


YEHOVA-YIRE ²

 Zikomo inu, M'bale Roy. Tiyeni tikhale chiyimire kwa mphindi yokha pamene ife tikupemphera. Ife tiweramitse mitu yathu, ngati inu mungathe. Ndipo tiyeni tingoganiza tsopano ngati muli chirichonse mu mtima mwanu chimene inu mungafune kuti Mulungu akuyankheni, usikuuno, chopempha china, mungolola icho chidziwike pamene mukukweza dzanja lanu, ndikuti, "Ndiri ndi chopempha pamaso pa Mulungu." Tsopano tiyeni ife tiweramitse mitu yathu pamene ife tikupemphera.

² Atate athu Akumwamba, ife tikuwutenga uwu mwayi waukulu, kuti tibwere kwa Inu; podziwa ichi, kuti ngati ife tibwera mu Dzina la Ambuye Yesu, ife tinalonjezedwa kuti tidzalandira chimene tachipempha. Tsopano sitikubwera ku Mpando Wachiweruzo. Ife ndithudi sitingafune kubwera kumeneko, kapena ku Mpandowachifumu wa Chirungamo. Koma ife...tikubwera ku Mpandowachifumu Wachifundo, kumene ife tiri—tikutsimikiza kuti zopempha zathu ziperekedwa. Pakuti, ife sitingapirire chiweruzo Chanu, komanso ife sitingakhale moyo ndi chirungamo Chanu, koma chifundo Chanu ndi chimene ife tikupempha. Mutikhululukire ife ndiye, Ambuye, a machimo athu. Ife tikupemphera kuti Inu mupereke zimenezo, ndipo kuti Inu mukhale ndi ife usikuuno, kuyankha pempho lirilonse limene manja amenewo amachiimirira pamene iwo amakwezedwa mmwamba. Inu mukudziwa chimene chinali pansu pa dzanjalo, mu mtima. Ndipo, Mulungu, sindikukaikira izo zinali chifukwa cha matenda, ndi chipulumutso, ndi okondedwa. Ife tikupemphera usikuuno, Atate, makamaka chifukwa cha iwo, kuti Inu mupereke zopempha zawo.

³ Tsopano ife takhala tikuyankhula pa wantchito Wanu wokhulupirika, Abrahamu, tikupitiriza ndi iye usikuuno, mu ulendo wake. Ife tikupemphera kuti Inu mutidalitse ife pamene ife tikupita mu njira ya mahandirede ambiri a zaka zapitazo, ndi wantchito wokhulupirika amene anakhulupirira Mawu Anu. Mulole icho chikhale chitsanzo, monga Paulo ananenera mu Ahebri, za chimene Abrahamu anali, chitsanzo. Ndipo ife tikupemphera kuti iye, chikhulupiriro chimene iye anali nacho, chiwululidwe kwa ife usikuuno; kukhulupirira Mawu a Mulungu, ndi kusawakayikira Iwo, Mawu amodzi a Iwo, koma kuwakhulupirira Iwo onse, ndi kukhulupirira chirichonse chimene Iye ananena. Ndipo mulole ife tithe kugwiritsitsa malonjezano amene Iye watipangira ife, ndi kukhala ana a Abrahamu mwa kukhala mwa Khristu. Ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

Khalani pansi.

⁴ M'bale Borders ndi wamtali pang'ono kuposa ine, chotero ine ndikuyenera kuwatsitsa maikrofoni mmusi pang'ono. Ndipo ndi chamwayi kukhala pano usikuuno mu msonkhano uno kachiwiri, ndi kudzapempherera odwala, ndi kudzachita chirichonse chimene Mzimu Woyera ukutiya ife kuti tichite. Ine ndikufuna ndinene ichi, moyamikira. Pa maulendo anga onse kudutsa mu U.S., United States ndi Canada, ine ndinawona chinachake usiku wathawu chimene chinandikondoweza ine mochulukwa kuposa mipando yamagudumu yonse imene ndakhala ndikuiwona ikukuthulidwa, ndi ndodo zonse zikutayidwa pansi, akhungu kupenya, ogontha kumva, osayankhula kuyankhula, akufa kuwukitsidwa, adotolo anasaina chi pepala kuti “munthuyo anali wakufa, ndipo anawuka.” Zonsezo zakhala zokondoweza. Koma pamene ndinawawona anthu usiku watha, amene ali mamembala a mpingowu, akulandira Choonadi ndi kuyimirira pakati pomwe pa anthu, kudzavomereza kuti iwo akulakwitsa ndi kulolera kuti azichita zolondola, izo zinali zopambana zimene ine ndikuzidziwa.

⁵ Mpingo, mwinamwake Mkwatibwi wasankhidwa kale. Ndiko, wamukonzekeretsa Iye tsopano. Kumupeza Iye . . .

⁶ Chitsitsimutso chatha. Ife tikudziwa zimenezo. Palibenso mzimu wachitsitsimutso. Maora awiri a utumiki, aliyense akudandaula. Mu chitsitsimutso, ndi usana ndi usiku, nthawi zonse, osapumulira. Chitsitsimutso chatha. Ndipo chotero ife tikungokunkha basi.

⁷ Abrahamu anachita kukhetsera thukuta mpaka atapeza khalidwe. Ndiyeno pamene iye anapeza khalidwe, chinthu chotsatira chinali kumukonzekeretsa iye ndiye kuti akakomane ndi mkwati. Ndicho chinthu chotsatira. Inu mukukumbukira pamene iye anamupeza iye? Nthawi ya kumadzulo, kuwala kwa kumadzulo.

⁸ Kukantha pa akazi ndi amuna, awiri onse, usiku wathawu; ndipo kuwawona iwo, polemekeza Mawu, akuimirira ndi kuvomereza kuti iwo akulakwitsa, akufuna chikhululukiro cha Mulungu, ndi kumapitirira chitsogolo; malo ake ndi ano okhalira ndi chitsitsimutso. Ngati pangakhale chitsitsimutso chirichonse chimene ine ndikuchidziwa, icho chidzachitikira pomwe pano, pamene mitima yowona! Chifukwa chiyani? Inu muli ndi chinachake choti muchigwirirepo ntchito, mwaona. Chinachake . . . Ambiri a iwo amakhala amwano, iwo samafuna kuti muwauze iwo za izo; mungokumbukira, mbewu ya mtundu umenewo ndi mbewu ya chipembedzo, osati Mbewu ya Abrahamu. Mbewu ya Abrahamu imawawona Mawu, ndipo iyo imawakhulupirira Mawu, mwamsanga.

⁹ Pamene hule laling’ono lija, pa chitsime usiku uja, mkazi wa pa chitsime...Kunali ansembe ndi aphunzitsi atayima mozungulira, akumuyang’ana Yesu akuchita, akupereka chizindikiro Chake cha Umesiya kwa iwo, chizindikiro cha Malemba, ndipo iwo anati, “Iye ndi Bezebule, mdierekezi, wam’bwebwe.”

¹⁰ Koma mwamsanga pamene Kuwala kuja kunadzawalira kwa mkazi wamng’ono uja, pamene Iye anamuuzza iye chimene iye anali atachita, iye anati, “Bwana, ine ndazindikira kuti Ndinu Mneneri. Ndipo ife tikudziwa kuti Mesiya akubwera, ndipo, pamene Iye abwera, Iye adzatiuza ife zinthu zimenezo.” Mwaona, mwamsanga Mbewu yokonzedweratu imeneyo inagwira izo, chifukwa iyo inali Mbewu ya Abrahamu, moonadi. Ndipo iye anakuwona Kuwala. Iwo anali Mawu. Iye ankadziwa kuti Mawu analonjeza kuti, pamene Mesiya adzabwera, Iye akanadzachita zinthu zimenezo, ndipo iye anazindikira izo.

Yesu anati, “Ine ndine Iye amene akuyankhula ndi iwe.”

¹¹ Iye anathamangira mu mzinda ndipo anayesetsa kukawakopa ena. Iye anati, “Bwerani, mudzamuwone Munthu Amene wandiuza ine zinthu zimene ine ndazichita. Kodi uyu si Mesiya kumene?” Mukuona?

¹² Tsopano mawu chabe kwa alongo athu. Nthawizonse ndimatengedwa ngati wodana ndi akazi, koma ine sindiri. Mukuona? Pamene ndinali mwana wamng’ono, ndinali ndi chondichitikira chopweteka; koma ine nthawizonse ndimakhala ndi ulemu waukulu kwa mkazi amene anali mkazi, dona. Koma sindimakhala ndi ulemu kwa iwo amene amadzinenera kuti ndi iwowo ndipo siali. Ine ndimakonda kuwona dona, dona weniweni wapachiyambi, iye ndi ngale.

¹³ Mu tsiku lino pamene akazi apotozedwa, opotozedwa kwambiri mmasiku otsiriza ano. Malemba amanena chomwecho. Chifukwa chiyani? Ndiko kutuluka kwa m’badwo. Inu mukukumbukira chimene chinali kupotoza koyamba? Anali mkazi. Uko nkulondola. Ndipo mu tsiku lotsiriza! Ife sitinayambe takhalapo ndi izi; takhalapo nazo zaka sikisi sauzande zimene madona anayesetsa kuti akhalabe madona. Tsopano iwo akuyesetsa kuti azichita monga mwamuna, kumavala zovala ngati mwamuna, kumadula tsitsi lawo ngati mwamuna, ndi zina zotero. Iwo sankachita konse zimenezo mu m’badwo wina uliwonse. Baibulo limaneneratu zimenezi, kuti iwo akanadzachita izi mmasiku otsiriza. Ndipo ndi inu apa, kupotozedwa kwa akazi. Nzosadabwitsa Baibulo linati, “Iwo amene anathawa kuchoka ku—kuchoka ku—kuchoka ku Ziyoni adzakhala aulemelo pamaso pa Ambuye, tsiku limenero.” Mwaona, momwe iwo amene anathawa!

¹⁴ Inu mukuti, “Izo sizimapanga kusintha kulikonse.” Izo zimapanga kusintha. Winawake ananena kwa ine osati kale

kwambiri, anati, “M’bale Branham, chinthu chaching’ono chimenecho sichimapanga kusintha.”

¹⁵ Ine ndinati, “Izo zinatero kwa Paulo. Ndipo Paulo anati, ‘Ngati mngelo wochokera Kumwamba abwera ndi kudzaphunzitsa china chirichonse, msiyeni iye akhale wotembereredwa.’ Kaya akhala mtumiki, kapena mngelo, kapena bishopu, papa, kapena chirichonse chimene iye ali, msiyeni iye akhale wotembereredwa ngati chirichonse chiri chosiyana ndi Ichi.” Mwaona, ndizo ndendende. Agalatiya 1:8, ngati inu mukufuna kuti muwerenge Iwo.

¹⁶ Ndipo iye anati, “Chabwino, ine sindikuganiza. . .” Anati, “Ine ndinawawona akazi okhala ndi tsitsi lalifupi, anali ofatsa basi ndi okoma.”

¹⁷ Ine ndinati, “Ndiko kulondola ndendende, ine ndinaziwonazo zimenezo. Koma izo sindizo. Mwaona, inu muzenera kubwera ku chimene Baibulo linanena!”

¹⁸ Bwanji ngati Mulungu akanati kwa Mose, “Vula nsapato zako,” ndipo iye ndikuti, “Ambuye, ndingovula chipewa changa, mmalo mwake”? Mukuona? Mukuyenera kuchita chimene Mulungu akuti muchite! Ndipo vuto lake linali, limene ine ndikuganiza, chimene chimandipangitsa ine kumadandaula kwambiri za izo, nkuti atumiki amalolera chinthu choterocho! Ndi chiyani chimenecho? Izo zimawonetsera kuti ndi Adamu wamakono amene wapita ndi mkazi wake. Mukuona? Mulungu akufuna Adamu wina amene angayime ndi Mawu, ndipo Iye yekha, Mawu okha. Mawu ndi olondola, mosalabidira! Musapite njira imeneyo.

¹⁹ Palibe, mu zaka sikisi sauzande, sipanayambe zachitikapo kuti akazi akhumbe kuti azimeta tsitsi lawo, kuvala ngati mwamuna, kupotozedwa. Ife tiri pa nthawi yotsiriza. Ndipo America, aliyense amene amadziwa ulosi, amadziwa kuti America amaimiridwa ndi mkazi. Izi zimatchedwa “ufulu wa amayi.” Ufulu wa chiyani? Kuchita zimene iye akufuna, tchimo.

²⁰ Mkazi sangachite zimene iye akufuna. Baibulo limanena kuti ayi. Mkazi ndi wochokera kwa mwamuna. Iye sali nkomwe mu chirengedwe chapachiyambi. Ndiko kulondola ndendende. Iye anatengedwa kuchokera kwa mwamuna. Mwamuna anali ziwiri zonse wamkazi ndi wamwamuna; Iye anatenga mzimu wachikazi ndipo anawuyika iwo m’nthiti imene inachokera kumbali yake. Mvetserani! Kodi inu munazindikira pamene Rebekah anapita kukakumana ndi Isaki, pamene analumphu pa ngamila, anaphimba nkhope yake? Chifukwa chiyani? Iye anali akubwera kwa mutu wake.

²¹ Iwo sakudziwa zimenezo. Iwo akuyenera kuchita zimenezo, mulimonse. Kodi inu munazindikira mkazi pamene akukwatiwa, iye amavala chophimba pa nkhope yake? Chifukwa chiyani? Iye akubwera kwa mutu wake. Ndipo Mpingo, Mpingo,

pokhala Mkwatibwi, uzidziphimba wokha ku kachikhulupiriro kalikonse, iwo ukubwera kwa Mutu wake, Mawu. Khristu ndi Mawu, ndipo Iye ndi Mutu.

²² Tsopano, abwenzi, ine sindikufuna kuti ndiyambe pa zimenezo. Ine—ine—ine ndimayang’ana uko lero, ndi malemba faivi handirede, abwinoko pang’ono kuposa malemba faivi handirede, a ziphunzitso zakuya za Baibulo. Koma ine ndikungofuna kuti ndikhale ndi Abrahamu pa msonkhano uno, mwanjira ina.

²³ Inu mukudziwa, ine ndikukhulupirira Ambuye akhoza, ngati abale sakusamala, ndipo ngati aliyense, ine ndikufuna kuti ndidzabwerere kuno ndi kudzachititsa chitsitsimutso kumene inu mungathe kukhala kanthawi, mwaona, pamene ife tingadzakhazikike pansi kwenikweni ndi kungowona. [Osonkhana akuwombera mmanja—Mkonzi]. Zikomo. Zikomo. Zikomo. Ndikudziwa kuli nsomba kuno, ine—ine—ine ndikudziwa zimenezo. Ndipo ndimakonda kuwedza. Ndipo muli ndi zipangizo zoti ukhoza kugwira nazo ntchito, winawake amene ali woonamtima. Aliyense akhoza kulakwitsa. Inu simukudziwa; ine ndimafa tsiku ndi tsiku, kuchokera ku zolakwitsa zanga, ndipo ndimayesetsa kukhala moyo pamaso pa Khristu. Ndipo aliyense amene ali wamkulu mokwanira, ndipo ali ndi Mzimu wa Mulungu wokwanira kuti aziyenda ndi kumavomereza kuti walakwitsa, kunena kuti, “Ine ndikufuna chinthu cholondola,” ine ndingakhale ndi chidaliro chochuluka pamenepo, pakuti, imeneyo ndi moonadi Mbewu ya Abrahamu. Iwo akufuna kuti awadziwe Iwo. Iwo sangawadziwe Iwo pokhapokha iwo atawamva Iwo. Koma Iwo akuyenera kuti amvedwe kaye poyamba, anati, “Momwe ife...popanda mlaliki? Ndipo mlaliki angalalikire bwanji ngati Mulungu sanamutume iye?” Ndizo ndendende Choonadi. Tsopano, zindikirani tsopano.

²⁴ Ife tikubwerera kwa Abrahamu tsopano. Ife kulibwino tibwerere kwa iye, chomwecho, ndi kumapitirira nazo izo. Kodi inu mukundimva ine bwino, pamwamba pa khonde mmwamba uno? Ndife...Zabwino kuwona, usikuuno, gulu labwino chotero. Ndinu anthu okondeka kuno. Ine ndithudi...

²⁵ Ndimayankhula ndi mzanga lero, amene wabwera kuchokera ku Canada. Ambuye anali atanditsogolera ine kuti ndipite ku malo ena kumene ine ndimayenera kuti ndikawone chinachake choti chichitika. Ndiyeno nditayima... Mzanga uyu, ndinakumana naye iye, ndipo iye amanena za mmene anthu a ku America anali ochezeka. Ndipo ine ndinati, “Inde, ndipo muno muli ina ya a—Mbewu yokonzedweratu ya Mulungu, mkati ndi kuzungulira malo awa, ndi mmalo oyipa kwambiri awa.” Ine sindikutanthauza mzinda wanu kuno. Mzinda wanga, kumene ndimachokerako, ndi woyipa ngati wanu. Koma dziko lonse ndi loyipa, koma zinyalala zonse zayandama kumapita

Kumadzulo. Ife tikudziwa zimenezo. Chitukuko chayenda ndi izo. Ndipo kumene kuli chitukuko, uko ndi kumene tchimo limakhalako. Izo nzoona. Muyang'ane izo mmwamba ndi pansi apa. Awa ndi manda a mlaliki. Uko nkulondola. Tayang'anani pa Los Angeles, chirichonse ndi mwambo uliwonse umafikira kumeneko, ndipo aliyense ali ndi kachikhulupiriro, chiphunzitso. Kuti atengere Mawu mmenemo, inu simungakhoze kuchita zimenezo. Izo zayipitsidwa kwambiri! Uko nkulondola. Ziwanda, adierekezi, pampando kumene pa Satana! Komabe pakati pa zonsezo, muli Mbewu ina mmenemo, aponso. Ndipo chinthu chokhacho chimene inu mungachite ndi kumwaza Kuwala. Ndipo ngati kalikonse ka Kuwala kumeneko. . . Ngati muli Mbewu mmenemo, iyo idzabwera ku Moyo mwamsanga pamene Kuwala kukhudza iyo. Inu mukungoyenera kufesa Kuwala, ndizo zonse. Ndipo Iye ndi Kuwala kwa kumadzulo, ife tikudziwa zimenezo, Mawu Ake.

²⁶ Tsopano, usiku watha ife tinamusiya Abrahamu. Ine ndinayambira pa—pa mutu wa 22, koma ine sindinaumalize iwo, chifukwa ine ndinapita kukakhazikika pa chimene Abrahamu anali pachiyambi. Ndipo ife tinamusiya iye usiku watha pamene Mulungu amatimikizira pangano ndi iye. Oh, ine ndikuzikonda zimenezo. Kumung'amba mwiniwakeyo, kupanga a—pangano ndi Abrahamu. Ndipo momwe ife tinapezera. . . Pamene Iye anamuyitana Abrahamu, ndipo ankati akatsimikizire pangano kwa iye, Iye anamuuzza iye kuti atenge nyama zitatu za zaka zitatu, ndi kuzilekanitsa izo. Ndipo ife tiri ndi zitatu. Ife tiribe nthawi yoti tilowe mu zimenezo. Mai, inu mukhoza kukhala pa ilo, phunziro limodzi limenelo pomwe apo, mpaka mmawa, osakhoza kulifotokoza ilo. Koma ukhoza kungokhala ngati kugunda malo okwerawo, ndi kuyembekezera Mzimu Woyera mu nthawi ino kuti uwulule zina zonsezo.

²⁷ Tsopano, momwe kuti ungwiro, Nsembe yangwiro, yangwiro, Mulungu anakhala wangwiro mmoyo wa munthu chimene Iye ankati adzachite. Ife tikudziwa kuti tatero. . . Ife tinali ndi Mulungu Atate, amene anali Yehova Wamphamvuzonse. Kenako Iye anadzakhala mu Lawi la Moto, linamutengera Israeli kudutsa mchipululu. Ndipo Yehova yemweyo anasandulika thupi ndipo anadzakhala pakati pathu, mmawonekedwe a Mwana Wake wobadwa yekha, analenga Kachisi Wake wa Iye Mwini kuti adzakhalemo, Mulungu anawonetseredwa mu thupi. Chidzalo cha Umungu mthupi chinadzakhala mwa Iye, mawonetseredwe angwiro. Kenako (kudzera mu pangano) gawo la umunthu la Iye linadzachotsedwa, linadulidwa, kuti Iye adzathe (pangano ili) kulekanitsa Thupi limene linafa, Magazi amene anakhetsedwa ku chikhululukiro cha machimo, ndipo analikweza Ilo mmwamba ndipo analikhazika Ilo pa dzanja Lake lamanja, ndipo anatomiza Mzimu kubwerera pa Tsiku la Pentekoste.

Ndipo Moyo womwewo umene unkakhala mwa Khristu Yesu ukuyenera kumakhalidwa mwa anthu apangano, Moyo womwe womwewo ukuchita chinthu chomwe chomwe chomwecho. Yesu ananena mu Yohane 14:12, “Iye amene akhulupirira pa Ine, ntchito zimene Ine ndikuzichita iyenso adzazichita.” Tsopano, izo mwina ndi zolondola kapena zolakwika. Izo zikuyenera kukhala zolondola! Kwa ine, Mawu aliwonse a Iwo ndi olondola. Mawu aliwonse ndi olondola mwangwirowo. Zindikirani momwe mwaulemerero Mulungu amagwirira ntchito.

²⁸ Ndipo kenako momwe iwo a Atate...Monga Mateyu ananena, “Pitani inu chotero, kaphanzitseni mafuko onse, kuwabatiza iwo mu Dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.” Mukuona? Tsopano, Atate...Sizikutanthauza kuti tiri ndi Milungu itatu. Ife tiri ndi Mulungu mmodzi mu maudindo atatu (Utate, Umwana, Mzimu Woyera), Mulungu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndizo ndendende.

²⁹ Tsopano zindikirani momwe mwaulemerero izo zinawonetseredwa kwa Abrahamu, ndi momwe kuti Mulungu, mu Kuwala uku, anapita pakati pa zibanthu izi, kuziduladula izo. Monga ngati...Tinazitenga usiku wathawu, momwe iwo ankapangira mgwirizano, ankalemba ndipo kenako amang’amba, kuti izo zilumikizane. Mgwirizano woukuyenera kugwirizana.

³⁰ Tsopano inu mukuona, abwenzi, ndicho chimene ine ndikuyesera kuti ndinene. Ngakhale pakati pa anthu athu Achipentekoste, pakubwera mdierekezi uyu wa luntha, akuyesetsa kuti awapange anthu...Tsopano, ine ndimakhulupirira mu mphatso zonse za Mulungu. Ine ndimakhulupirira mu kufuula. Ine ndimakhulupirira mu kuyankhula ndi malirime. Ine ndimakhulupirira mu zinthu zonse zimene Mulungu ananena. Koma komabe inu simungadalire pa chirichonse cha zinthu zimenezo kukhala chifukwa chimene inu munalandirira Mzimu Woyera. Mwaona, moyo wanu uyenera kupita nazo izo. Mukuona? Zanu... “Ndi zipatso zanu inu mumadziwika.” Mukuona? Ndipo izo ndi zinthu zimene zimandidetsa nkhawa ine lero, chifukwa ine ndimawuwona mpingo wanga womwe, mpingo wa Chipentekoste, ukukhala nawo “mawonekedwe aumulungu,” kuchoka ku Choonadi. Ndipo ukabwetsa Choonadi cha Mawu kwa iwo, iwo amachoka kwa Icho. Kenako ukawapempha iwo, “Bwerani, mudzakhale ndi ine,” iwo sangachite izo. Mwaona, izo zimasonyeza kuti pali chinachake cholakwika. Ndi zimene zimandidandaulitsa ine. Ndipo, tsopano, izo sikuti ine ndikutsutsana ndi mpingo wanga. Ndine... .

³¹ Ngati ndimamukonda Khristu, zingakhale zabwino kwambiri kuti ndizibwekerera za Mpingo Wake kusiyana ndikuti ndizibwekerera za Iye. Chifukwa ine ndingakonde kuti muzibwekerera za ana anga kuposa kuti muzibwekerera

za ine. Ndipo, kumbukirani, kawirikawiri ine ndimaganiza, ngati ndikanakhala ndi madontho awiri a Magazi enieni a Yesu mu mbale, momwe ine ndikanawagwirira Iwo, kuti ndisawataye Iwo. Ndikanayenda mosamalitsa kwenikweni. Koma usikuuno ine ndiri ndi zazikulu kuposa zimenezo, pamaso Pake, ine ndiri ndi ogulidwa ndi Magazi Ake. Mwaona, Iye anakhetsa Magazi Ake chifukwa cha inu. Ndipo ine ndiri pano ngati mtumiki usikuuno, nditagwirizira, kapena kukulozerani inu kopita kwanu Kwamuyaya. Chotero ine sindilozera ku kachikhulupiriro kalikonse kapena mbalume iliyonse; iwo akuyenera kukhala Mawu, chifukwa ndicho chinthu chimene chitakhalitse. Chikhulupiriro changa chamangidwa pa Mawu, ndipo Khristu ndi Mawu. Ndipo ngati Khristu angapangidwe kukhala Mawu, ndiye kuti Mawu akuwonetseredwa pakati pathu pomwe. Mwaona, izo zikuyenera kutero!

³² Tsopano, chotero, ine ndikukhulupirira kuti Mulungu wa Chipangano Chakale, zonse zimene Iye anali, Iye anazitsanulira mwa Yesu Mwana Wake. Ndipo zonse zimene Yesu wa Chipangano Chatsopano anali, Iye anazitsanulira mu Mpingo umene Iye anawugula ndi Magazi Ake Omwe. Mukuona? “Kanthawi pang’ono ndipo dziko,” *kosmos* uko, dongosolo la dziko, “silidzandiwona Ine kenanso. Komabe inu mudzandiwona Ine,” *inu*, Mpingo, “pakuti Ine ndidzakhala ndi inu, ngakhale mwa inu, mpaka kumatsiriziro a dziko lapansi.” Ndiye Moyo, Mgwirizano uja, Mzimu uja umene unachotsedwa mwa Khristu pa Kalvare, wabweretsedwanso ndi kutsanuliridwa pansu pa anthu, Mbewu ya Abrahamu, imene Mulungu anayipangira lonjezo. Kumbukirani, sizinali kwa zimbewu zake zonse, koma “Mbewu.”

³³ Tsopano, pali chiphunzitsa cha kukonzedweratu chimene chiri chovunda, zamkutu. Koma pali kukonzedweratu kwenikweni kolondola. Mulungu, mwakudziwiratu, akanatha kukonzeratu chifukwa Iye amadziwiratu. Mulungu sakufuna kuti aliyense awonongeke, koma, pokhala Mulungu wopandamalire, ankadziwa amene adzawonongeke ndi amene sadzawonongeke.

³⁴ Ndi chifukwa chake Iye ananena Isaki kapena—kapena. . . Yakobo kapena Esau asanabadwe, Iye anamuda Esau ndipo anamukonda Yakobo. Kudziwiratu Kwake kunamupangitsa Iye kudziwa kuti Esau anali tambwali, ndipo Iye anamudziwitsa Iye kuti Yakobo ankalemekeza ufulu wakubadwa uwo; mosalabadira momwe iye anawupezera iwo, iye ankawufuna iwo. Tsopano, anyamata awiri onsewo, amapasa, obadwa kuchokera kwa amayi woyera yemweyo ndi abambo, koma wina anali chigawenga ndipo winayo anali a—wokhulupirira. Tsopano Mulungu, mwakudziwiratu Kwake, anadziwa zimenezo.

³⁵ Tsopano, Mulungu, mwakudziwiratu, Iye—Iye samaika

bizinesi Yake monga...Inu simungachite bizinesi yanu mwanjira imeneyo, patsamba lomasuka monga choncho. Mulungu ankadziwa, mwakudziwiratu, amene akanati adzapulumutsidwe, chotero Iye anatumiza Yesu kuti adzawagwire iwo amene Iye anawawoneratu kuti akanadzapulumutsidwa. Muwerenge Aefeso, mutu wa 1, ndipo inu muziwona izo. Mukuona? Tsopano, pamene.

³⁶ Ndiye Iye anatsitsa Uthenga Wake ndipo akuwubzala Iwo, akutsitsa Mzimu Wake kuti adzawupangitse Iwo kukhala wamoyo. Tsopano, izo zonse zidzakulira mmunda womwewo, Ahebri 6 amatiuza ife zimenezo, “Kuti mvula imabwera mowirikiza,” Yesu anati, “padziko lapansi,” ndipo muzindikira pamene, “kudzakonzekeretsa, kudzalikonza dziko lapansi; koma minga ndi nthula, zimene ziri pafupi kukanidwa, zomwe mapeto ake ndi kuwotchedwa.” Mwazipeza izo? Tsopano kumbukirani.

³⁷ Ife titenga munda wa tirigu. Anthu inu mumalima tirigu kuno. Ndipo apa pali a—chilala chinabwera. Apa pali zoyanga kapena udzu umene muli nawo pano, udzu wina wodziwika umene ukumera mmunda; zoyanga mmunda, namsongole mu gudumu . . . mmunda, nthula mmunda. Ndipo tirigu ali mmunda. Zonse ziri ndi ludzu. Ndipo mvula siimabwerera namsongole, koma tirigu, koma udzu waung’ono umenewo umaimirira ndi kusangalala mochulukira basi monga tirigu angachitire.

³⁸ Koma ndi zipatso zawo inu mumadziwika. Mzimu womwewo umagwera pa wachinyengo ndipo iye amafuula ndi kupapitirira monga ena onsewo, koma moyo wake ndi umene umatsimikizira chimene iye ali. Mukuona? Ndipo timadalira kwambiri zogirigisha. Ndipo lero munda wadzadza ndi mitundu yonse ya zogirigisha, mtundu uliwonse wa kugirigisha wopanda malemba ndi china chirichonse. Ndithudi. Koma ife tikuyenera kubwerera ku Mawu, Choonadi cha Mawu. Mawu, chimene Iwo ananena!

³⁹ Tsopano, Mulungu akumuza Abrahamu kuti kudzera mwa iye, pangano lachitatu, ndipo pangano lokhalo. Yesu yekha anali chitsimikiziro cha pangano limene Iye anapangana ndi Abrahamu, Mbewu yachifumu, Mbewu ya Mzimu.

⁴⁰ Ndipo kwa inu abwenzi anga ofunika Achikatolika, pamene inu munena kuti, “Tikuoneni, Mariya, amayi a Mulungu,” kodi inu simumachita manyazi? Kodi zingatheke bwanji kuti Mariya akhale mayi wa Mulungu? Iye sizingatheke kuti akhale. Inu mukuti, chabwino . . .

⁴¹ Ine ndimayankhula ndi winawake tsiku lina, iwo amatsutsana. Iwo ananena kuti—kuti Yesu anali—mbewu ya—ya Mariya. Ngati Iye anali mbewu ya Mariya; mbewuyo isanatsike kudutsa mu thumbo, pankayenera kukhala kugirigisha kumene

kukanaibweretsa iyo. Ndiye kuti mukumupanga Yehova... Inu mukuona chimene inu mukumupangitsa Iye kuchita?

⁴² Mulungu, Mlengi, analenga ziwiri zonse dzira ndi khungu la Magazi, ndipo anabweretsa Kachisi. Ndipo munthu analibe chochita nazo Izo! Anali Mulungu yekha! Uko nkulondola.

⁴³ Iye anali mkazi wabwino, ndithudi. Alipo abwino ambiri akhala pano usikuuno. Ndipo pamene Mulungu atsiriza kugwiritsa ntchito chirichonse, icho chimachoka pamalo. Ndipo mkaziyo si mkhalapakati. Iye si mayi a Mulungu. Iye ndi mkazi wabwino, woyera mu Ulemelero, chifukwa iye anatumikira cholinga cha Mulungu. Ndipo mkazi aliyense muno ali nawo mwayi womwewo, mwinamwake osati mwanjira yomweyo, koma kuti azitumikira Mulungu. Mukuona? Mulungu adzakugwiritsani inu ntchito.

⁴⁴ Iye anangomugwiritsa iye ntchito ngati chofungatira, koma Mwanayo anali wa Mulungu. Eya, Iye anali Mlengi wa ziwiri zonse dzira ndi magazi amoyo. Ndipo magazi amoyo, ndithudi, amabwira kuchokera kwa mwamuna; ndipo Iye anali Mlengi wa zimenezo. Ndipo Mariya anapatsidwa mwana uyu popanda kugirigisha kulikonse, osati wina kuposa Mzimu Woyera utamuphimba iye ndi kulenga mu chiberekero chake khungu la Magazi ili ndi dzira zimene zinabereka Mwamunayo, Khristu Yesu.

⁴⁵ Ndipo limenero linali pangano limene Mulungu ankalembe nalo, kuti pamene Mulungu anapangidwa munthu pakati pathu, ndiye Iye anang'ambidwa pakati. Mwaona, atatu a iwo, wa usinkhu wa zaka zitatu, ndiye anang'ambidwa pakati. Ndipo Mulungu anatengera gawo limodzi la Ilo Kwawo ndi Iye, ndipo anatumiza gawo linalo panso pano. Tsopano pamene Thupi lidzakumananso, udzayenera udzakhale Moyo womwewo umene unkalumulira Thupi limenero ukuyenera kudzakhala Moyo womwewo ukulamulira Thupi ili. Ndipo Iye anali Mawu. Ndipo Iye ndi Mawu! Mukuona? Ndipo ntchito zimene Mawu ankachita kumeneko akuchita chinthu chomwecho lero. Iye ndi Mawu, Mawu Amuyaya. Ndipo Mawu a Mulungu ndi Amuyaya. Chabwino.

⁴⁶ Tsopano kodi Iye ankachita chiyani? Amapanga njira, kuwonetsera, kudziwa kuti Israeli, mbewu yachibadwa, ikanadzamukana Iye; koma podziwa kuti Mbewu yachifumu, osati kuchokera mu kugonana ndi Sarah, koma kuchokera ku chikhulupiriro chimene Abrahamu anali nacho, imene inabereka Khristu, ndiyo Mbewu yachifumu ya mafuko onse, osakanizidwa, Mkwatibwi akubwera kuchokera ku mafuko onse. Abrahamu, atate wa mafuko, osati chifukwa iye anali ndi... ankakhala ndi mkazi wake, Sarah, ndipo anabereka mwana wamwamuna, koma chifukwa iye ankakhulupirira Mawu. Amen. Ndi zimenezotu.

47 Tsopano ife tikupeza, zitatha izi, chochitika chachikulu ichi. Tsopano tikubwera ku mutu wa 17. Ife tiyesetsa kuti tipeze ya 22, ngati nkotheke. Mutu wa 17. Kodi inu mukuwukonda ulendowu ndi Abrahamu? Ine ndimangokonda kuziwona izo. Chifukwa chiyani? Chirichonse chimene iye anachita chinali choyimira changwirowo cha Mpingo. Inu mukukhulupirira zimenezo? Zindikirani, Malemba onse amaimira zimenezo.

48 Tayang'anani pa Yoweli, anati, "Izo zidzafika pochitika mmasiku otsiriza, kuti Mulungu adzatsanulira Mzimu Wake." Momwe kuti kudwabwera chimbalanga ndipo chidzadya mpingo Wake! "Chimene chirimamine chinasiya, chimbalanga; ndi chimbalanga, anoni." Ndipo ndi kachilombo komweko, chiwala chomwecho mmagawo anayi osiyanasiyana. Kalikonse kamadya gawo lake. Apa pakubwera anoni wakale kapena chimbalanga ndi kudzadya makungwawo, ndipo china chinadya chipatsocho, ndipo—ndipo kenako nkubwera motsatira zinazo zimene zinayamwa moyo kuchokera mmenemo. Pamenepo ndi pamene. . .

49 Khristu, Mtengo uwo umene unali mmunda wa Edeni! Panali mitengo iwiri mmunda wa Edeni. Mitengo iwiri iyi inayikidwa pamene ndi cholinga chakubala. Ndipo pamene. . .Eva, iye anali mtengo wa imfa ngati iye akanakhudzidwa. Ndipo Khristu anali Mtengo wa Moyo. Tsopano mwa mkazi imfa imabwera; mwa Mwamuna Moyo umabwera.

50 Tsopano pamene Iye anayima apa kumayankhula ndi Ayuda, Iye anati, "Ine. . .wanu. . ."

51 Iwo anati, "Makolo athu anadya mana mchipululu kwa zaka forte."

52 Iye anati, "Ndipo iwo ali, aliyense, wakufa! Koma Ine ndi Mkate wa Moyo, Mtengo wa Moyo, wochokera kwa Mulungu kuchokera Kumwamba, kuti munthu akadya Mkate uwo ndipo sadzafa konse."

53 Mulungu anayika Aserafi pamene, akulondera Mtengo umenewo, kuti wina asawukhudze Iwo. Tsopano Iye anawatulutsa Aserafi, kuyesetsa kuti awapitiki sire iwo ku Mtengo. Tsiku limenero, iwo anawona masomphenya, iwo ankafuna ku Mtengowo, kuti abwerere opanda chitetezero. Koma tsopano chitetezero chitapangidwa, mdierekezi akuwachititsa iwo khungu, kuwatembenezira iwo mbali iyi kuchoka ku Mtengowo. Zindikirani.

54 Pamene Khristu anabwera padziko lapansi, Iye anali Mtengo wangwirowo wa Mulungu. Davide anamuwona Iye mu Salmo ya 1, anati, "Mtengo wobzalidwa mmphepete mwa mtsinje, mitsinje ya madzi." Mitsinje yambiri, Madzi amodzi; mphatso zambiri, Mzimu womwewo. "Masamba ake sadzafota."

55 Koma pamene Iye anabwera pa dziko lapansi, chinachitika ndi chiyani? Mphamvu ya Chiroma inadulira mtengo umenewo

pansi ndipo inamupachika Iye pa mtengo wopangidwa ndi munthu. Kenako Mulungu anaukweza Mtengo umenewo ndipo anawuyika Iwo pa dzanja lamanja, ndipo anatumiza Mzimu kubwerera kuti udzamupangire Iye Mkwatibwi, monga mmene Adamu ankayenera kukhalira mmunda wa Edeni. Ndipo pamene mtengo umenewo unayamba, iwo unali mtengo wa chipentekoste.

⁵⁶ Timamva papa akunena kuti, “Mipingo yonse, bwererani ku manthu wa mpingo, ku chiyambi. Kubwerera ku Roma!”

⁵⁷ Ine ndikufuna wa zambiriyakale mmodzi, mtumiki mmodzi, kapena winawake kuti ayime, andiyang’ane ine munkhope ndipo andisonyeze ine kuti mpingo unayambira ku Roma. Mpingo unayambira ku Yerusalemu pa Tsiku la Pentekoste! Ndi kumeneko. Mabungwe anayambira ku Roma, zaka firii handiredede ndi chakuti mtsogolo. Koma Mpingo unayambira pa Pentekoste; Mulungu akuukitsa mtengo wa Mkwatibwi wa Khristu, ndi Mzimu womwewo umene unali mwa Khristu, kuwukitsa mtengo wa Mkwatibwi. Ndipo chinachitika ndi chiyani? Pamene iwo unayamba kubuula, kukula, kachilombo ka Chiroma kanafika pa iwo ndipo kanayamba kuswa iwo. Chimene chimbalinga chinasiya, anoni anadya, mpaka iwo unafika ku chitsa.

⁵⁸ Koma Mulungu anati, “Ine ndidzabwezeretsa, atero Ambuye.” Mtengo umenewo udzaphukiranso, pakuti Mtengo wa Mkwatibwi ukumutsatira Mkwatibwi.

Kenako panadzabwera Luther, kodi Iye anachita chiyani? Kutsatira kulungamitsidwa.

⁵⁹ Ndizo ndendende momwe mpingo unadzabwereramo, Yohane akulalikira kulungamitsidwa. Khristu anadzabwera, akulalikira kuyeretsedwa. Ahebri... Ine ndikutanthauza Yohane Woyera 17:17, “Ayeretseni iwo kupyolera mu Choonadi, Atate. Mawu Anu ndi Choonadi.” Ndipo Iye anali Mawu. Uko nkulondola. Iye anali Nsembe. Ndiye, pa Tsiku la Pentekoste, ndi Mzimu Woyera. Kulungamitsidwa; kuyeretsedwa; ndipo pamene mtengo unalandira ubatizo wa Mzimu Woyera, iwo unali mtengo wa Mkwatibwi wathunthu!

⁶⁰ Achiroma anawudya iwo. Basi pamene iwo unkapita pansu, iwo unadzatulukira! Ndipo pamene iwo unkayamba kubwera kupyolera mwa Luther, chiyani? Imfa ya Luther itachitika, iwo anapanga bungwe. Kodi Mwamunayo anachita chiyani? Anadula nthambi zakale zakufazo.

⁶¹ Anapita kutali, kutali, mtima wa mtengo ukukula. Ndi mtengo wokonzedweratu! Mbewu imeneyo yagona pamene, iyo ikuyenera kubwera! Ndipo kukwera iwo unabwera kachiwiri, ndipo Wesley anayamba. Ndipo iwo anali ndi chitsitsimutso chachikulu pansu pa kuyeretsedwa. Chinachitika ndi chiyani? Iye anawudulira iwo kachiwiri, pamene iwo

anachita bungwe. Palibe bungwe linayamba lawukapo. Palibe limodzi limene linayamba lagwapo limene linabwerreranso.

⁶² Kenako motsatira panadzabwera Achipentekoste, ndi kubwezeretsa kwa mphatso. Kodi icho chinachita chiyani? Anapanga bungwe! Kodi Mulungu anachita chiyani? Anawudula iwo!

⁶³ Koma kodi Iye ananena chiyani? “Ine ndidzabwezeretsa, atero Ambuye.” Iye adzatulutsa kuchokera mu chisokonezeko chimenecho, Mpingo umene uli wotsukidwa ndi Magazi, wogulidwa ndi Baibulo, ndi wolimba mu Mawu, Mkwatibwi! Kuwala kwa madzulo kukutulukira. Kodi chipatso chimachera pati? Pamwamba pomwe pa mtengo. Apa ndikupitanso!

⁶⁴ Kubwerera kwa Abrahamu, tibwerere, tiyeni tifike kwa Abrahamu. Apa Iye akubwera, Mbewu yachifumu ya nthawi yamakudzulo ikubwera. Mafuko... Zindikirani tsopano ukatha mutu wa 17, ife tikupeza apa mu mutu wa 17, Mulungu anawonekera kwa Abrahamu mu Dzina la Mulungu Wamphamvuzonse.

⁶⁵ Abrahamu anali wa usinkhu wa zaka nainte ndi naini zakubadwa, ndipo nthawi yonse anali asanagwedezeke konse, koma ankakhulupirira Mawu a Mulungu; ndipo ankazitcha zinthu zimene kunalibe ngati kuti zinaliko, chifukwa Mulungu ananena chomwecho, akukhulupirirabe kuti mwana ameneyo akanadzabwera, akugwiritsitsa kwa lonjezo. Ndi munthu wotani! Ndi m’bale wotani! “Abrahamu, amene motsutsana ndi chiyembekezo...” Chiberekero cha Sarah chinali chakufa. Iye anali wosabereka. Thupi lake lakufa. Baibulo linati ilo linali, kuti thupi lake linali ngati lakufa. Ndipo chiberekero cha Sarah chinali chakufa. Ndipo iye anali tsopano pafupifupi zaka forte atadutsa kusintha kwa thupi, ndipo komabe Abrahamu ankakhulupirira izo, kuti iye adzakhala ndi mwana chifukwa Mulungu ananena chomwecho. Ndi zimenezotu. Kugwiritsitsa ku Mawu chifukwa Mulungu ananena chomwecho! Ziribe kanthu, tizikhulupiriro timene tinaphimba Iwo, ndipo, komabe Mawu amenewo anali pamenepo! Iwo ankayenera kubwera. Ndipo Mawu amenewo ali mu mtima wa Abrahamu!

⁶⁶ Zinalibe kanthu kuti ndi ochuluka bwanji amati, “Masiku a *izi* anapita, ndi *izo* apo.” Bola ngati Mawu amenewo ali pamenepo, iwo adzakhala olenga, chifukwa iwo ndi Mawu ophuka. Pakuti, Mulungu ndi Mawu, ndipo Moyo wa Mulungu umakhala mu Mawu. Zindikirani tsopano pamene Mawu amenewo agwera mu Moyo wa Mulungu, chinachake chimachitika, icho chimadzakwaniritsidwa. Tsopano zindikirani.

⁶⁷ Kenako Iye anawonekera kwa iye mu Dzina la Mulungu Wamphamvuzonse. Tsopano, Mulungu ali ndi mayina seveni a chiwombolo. Ndipo Iye anawonekera kwa iye

apa mmawonekedwe a Mulungu Wamphamvuzonse, zimene zimatanthauza “El Shaddai.” Mu... “Shaddai,” mu Chihebri. *El* amatanthauza “wamphamvuyo.” *Shad* amatanthauza “bere,” ngati bere la mkazi. Ndipo tsopano mmalo mokhala “shad,” chimodzi; “Shaddai,” zambiri. Tsopano ndi chitonthozo chokoma bwanji kwa munthu wokalamba, wa zaka handirede, akugwiritsitsa Mawu a Mulungu mu mtima mwake, ndipo apa Liwu la Mulungu likubwera kwa iye ndipo linati, “Ndine El Shaddai. Ndine Mulungu wa Mabere.”

⁶⁸ Oh, ndi chitonthozo bwanji chimene ife tiri nacho! Tsopano, osati, kumbukirani, osati chabe “bere,” koma “wamabere”! “Anavulazidwa chifukwa cha zolakwa zathu; ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.”

⁶⁹ Tsopano, kodi mayi amatani, ndi mwana wake wamng’ono, pamene iye akudwala ndi kudandaula? Iye amamunyamula mwana wamng’ono. Iwo amamunyamula iye pa bere lake, ndipo iwo... iye amayamwa mphamvu ya amake kulowa mthupi mwake kudzera pa berelo. Ndipo sikuti iye amangokhutitsidwa kapena iye... Iye amatontholetsedwa. Iye amafuula pamwamba pa mawu ake, iye amakhala yense wosokonezeka; koma pamene amayi amunyamula ndi kumuyika iye... kumuyika iye pa bere lake, ndi kuyamba kung’ung’uza kwa iye, kumugwedeza iye mmbuyo ndi mtsogolo, iye amawamverera amayi ake, mutu wake umakhala pachifuwa chawo, ndipo amayamba kuyamwa ndi kukoka mphamvu kuchokera kwa amayi ake, kulowa mu thupi lake. Iye akudzitsitsimutsa yekha, akumangirira mphamvu; komanso kukhutitsidwa, pamene tsiku ndi tsiku akukula mwamphamvu ndi mwamphamvu.

⁷⁰ Ndi chokuchitikira bwanji kwa Mbewu ya Abrahamu! Iye akanali Mulungu Wamphamvuzonse, El Shaddai! Ife tikhoza kugwira lonjezo lirilonse limene Iye anapanga mu Baibulo. Mbewu Yake, ana Ake, ngati inu mukudwala, mungogwira bere la lonjezo la Mawu amene anati, “Ndi mikwingwirima Yake ife tinachiritsidwa.” Izo zimakhutitsa! Ndipo ife tikukoka mowirikiza, mphamvu yathu, kuchokera kwa Wamphamvuyo, El, Wamphamvuyo, Wamuyayayo, kukoka Moyo Wake kuchokera kwa Iye, kudzera mu lonjezo Lake.

⁷¹ Ndikumverera kotani kumene kumampatsa munthu atagona pachifuwa cha El Shaddai, akukhulupirira, akudziwa kuti tikuyamwa mphamvu ya Khristu kuchokera ku lonjezo Lake, kulowa mwa ife!

⁷² Pamene El Shaddai anamutsamiritsa Abrahamu pa chifuwa Chake, zaka twente-faivi mmbuyomo; bambo wokalamba, usinkhu wa zaka sevente-faivi, ndi mkazi wake sikisite-faivi; iye sanasiye Bere limenelo. Iye anayenda mpaka kudutsa dziko lachilendo, pakati pa anthu achilendo amene sankamudziwa Mulungu, koma iye ankachitira umboni mosalekeza ndipo

anali wolimba mu chikhulupiriro, akupereka matamando kwa Mulungu, chifukwa iye ankadziwa kuti iye anakakoka kuchokera ku lonjezo limenero.

⁷³ Ndi chiyembekezo chotani chimene chiri kwa mpingo usikuuno, mu ora la mdima, zamatsenga, zogirigisha, zaluntha. Mzimu Woyera unati, “Mmasiku otsiriza padzabwera mpingo waluntha. Mzimu ukuyankhula mofotokoza,” Timoteo Woyamba 3, “mmasiku otsiriza ena adzachoka ku Chikhulupiriro, azidzamvetsera ku mizimu yosocheretsa, ndi ziphunzitso za ziwanda,” ndithudi, “okhala nawo mawonekedwe aumulungu.” Kodi iwo ankatani? “Aliuma, odzikweza.” Dokotala Ph.D., LL.D., QST, maudindo onsewa. “Bwanji, Dokotala *Wakuti-ndi-wakuti*, nthawi *yakuti-ndi-yakuti*, ndi abusa athu.”

⁷⁴ Ine ndingakonde mwamuna wina atakhala m’banja langa, kapena mwana wanga, amene sankadziwa kusiyana kwa pakati pa nyemba zogamphuka ndi khofi, ndipo nkumamudziwa Khristu! Uko nkulondola. Kumutengera iye kunjwa uko kwina kwake pafupi ndi chitsa chakale ndi kugwada pansa pa maondo ake ndi kupemphera ndi iye mpaka Mzimu Woyera utabwera mwa iye. Ine ndingakonde nditakhala ndi zimenezo kuposa zowerenga maganizo zonse zimene inu mungatsanulire mwa iye ndi digiri ya udokotala. Kumuuza iye Mawu a Mulungu! Inde.

⁷⁵ “Koma aliuma, odzikweza, okonda zokondweretsa kuposa okonda Mulungu, osayanjanitsika, onenera zabodza, osadziletsa, ndi onyoza iwo amene ali abwino.”

⁷⁶ Oh, inu mukuti, “Iwo ndi Achikominisi.” Ayi, ayi! Iwo ndi otchedwa Akhristu.

⁷⁷ “Okhala nawo mawonekedwe aumulungu, koma kumakana Mphamvu yake, kwa oterowo chokaniko. Pakuti awa ndi iwo amene amapita nyumba ndi nyumba, akutsogolera akazi opusa, otsogozedwa ndi zilakolako za mitundu mitundu, osatha nkome kufika ku chidziwitso cha choonadi.” Uko nkulondola. Ndicho chimene icho chiri. Ndipo tikuliwona tsiku limenero.

⁷⁸ Ndipo ndi chithonhozo bwanji kwa wokhulupirira, kuti adzipatule yekha ku kusakhulupirira konse, tizikhulupiriro tawo tonse topanda umulungu, ziphunzitso zawo zonse zopanda umulungu, ndi kuyang’ana molunjika kwa Khristu ndi kutenga Mawu, ndi kugwiritsitsa ku Mawu amenewo mpaka inu mutawawona Iwo akuwonetseredwa. Ziribe kanthu mudikira nthawi yayitali bwanji, khalani pamenepo! Mulungu analonjeza zimenezo. Iye anakutsogolerani inu kwa izo, gwiritsitsani kwa izo! Khalani pamenepo. Musabweze izo. Khalani pomwepo. Ngati mukutsimikiza za izo, inu mukhala pamenepo. Koma ngati mukukaikira, mudzataya chaching’ono chirichonse. Nyani amagwira zinthu zonyezimira, koma chimbalangondo

chimagwira chake. Chotero, inu mukhalebe! Inde, gwiritsitsani, kugwira bwino!

⁷⁹ El Shaddai! Iye anati, “Ndine El Shaddai. Abrahamu, Ine ndine Wamphamvuyo. Ndiwe munthu wokalama. Iwe uli ndi zaka handirede tsopano, mphamvu zako zonse zapita; koma Ine ndi Mphamvu yako! Chiyembekezo chako chonse chapita; koma Ine ndi Chiyembekezo chako!”

⁸⁰ Oh, inu mukuvutika, usikuuno, kunja kuno ndi khansa ndi zinthu, kodi inu simukuwona kumene Mphamvu yanu imachokera? Osati kuchokera ku mpeni wa dokotala, koma kuchokera ku Mawu a Mulungu! “Ine ndi Gawo lako! Ine ndi Mphamvu yako! Iwe umakoka mphamvu zako kuchokera kwa Ine!”

⁸¹ Osati kunyozetsa dokotala tsopano; iye amachita gawo lake limene liri kwa iye. Koma Mulungu ndiye Mchiritsi. Palibe dokotala wa oparesoni, palibe dokotala, palibe mankhwala amene angachiritse. Ayi, bwana, iwo alibe mankhwala amodzi amene angachiritse. Tsopano, dokotala aliyense angakuuzeni zimenezo. Iwo amakhala ndi zothandizira, koma Mulungu ndiye Mchiritsi. Iwo akhoza kudula bala mu dzanja lanu, koma Mulungu ayenera kulichiza ilo. Iwo alibe kalikonse komangira minofu; ngati iwo akanamatero, iwo akanamuwumba munthu. Chotero inu mwaona, Mulungu ndi Mchiritsi. Inu mukhoza kuyika fupa, koma Mulungu akuyenera kulichiza ilo. Mulungu ndi Mchiritsi, “Ine ndi Ambuye amene ndimachiritsa matenda anu onse.” Ndipo simungawapangitse Mawu a Mulungu kunama; Iwo adzabwerera ku choonadi nthawi iliyonse, molunjika basi kubwerera. Inu simungawapangitse Iwo kunama.

⁸² Tsopano iwo amati Baibulo limadzitsutsa Lokha. Ine ndawafunsapo, ndi kuwauza amuna kuti ndiwapatsa malipiro a pachaka kumunda, ngati ndingathe, chirichonse chimene ine ndingathe kuchita, kuti andisonyeze ine mawu amodzi mu Baibulo amene amatsutsana ndi enawo. Uko nkulondola. Mulibemo mmenemo. Ndi chifukwa malingaliro anu achithupithupi amayang’ana izo momwe amachitira. Mzimu Woyera ndi Wotanthauzira Mawu amenewo. Mawu amenewo ndi owona, akhala pamodzi. Zonsezo ziri pamenepo ngati zidutswa zopangira chinthu chimodzi, koma zimatengera Mzimu Woyera kuti uziyike Izo pamodzi, kuwapanga Iwo chithunzi cha chiwombolo cha Mulungu ndi madalitso Ake kwa anthu Ake. Ameni. Ilo silimadzitsutsa lokha! Palibe Lemba limodzi, palibe ndime imodzi ya Ilo, imatsutsana ndi imzake. Ngati izo ziri, izo sizoyenera pepala limene zinalembedwapo, ndi zonyenga. Mulungu sachita chinyengo. Mulungu ndi woona, wolungama, woyera, woonamtima. Iye ndi Mulungu.

⁸³ Tsopano, pamene Abrahamu analandira mawu awa, kuti

“Ine ndine El Shaddai. Ndine Wopereka Mphamvu wako! Mkazi wako, chiberekero chake chinauma kale, iye ali ndi zaka forte kudutsa kusinthika kwa thupi, thupi lako liri ngati lakufa; koma Ine ndine El Shaddai.” Iye anangomubweretsa Ishmaeli, inu mukudziwa; koma Iye anati, “Ameneyo si iye. Ayi, iye adzakhala munthu wopambana. Iye adzabala akalonga ambiri. Koma amene Ine ndinapanga naye lonjezo, ali pakati pa iwe ndi Sarah.” Ndi zimenezotu! Amen. Abrahamu anamverera bwino kwambiri.

⁸⁴ Iye anati, “Tsopano Ine ndikufuna ndikuuze iwe chinachake, Abrahamu. Ine ndikusintha dzina lako.” Iye anati, “Iwe sudzatchedwanso Abram, koma Abrahamu.” *Abramu* amatanthauza “wapamwamba—bambo wapamwamba.” Koma *Abrahamu* amatanthauza “atate wa mafuko.” Ndipo osatinso S-a-r-a-i; iye ndi S-a-r-a-h, *Sarah*, “mfumukazi.” Anasintha dzina lawo! Ndi a—dzina losinthidwa bwanji! Chinachake chinachitika chifukwa iwo ndi . . . Mwaona, pakuyenera kukhala kusintha zinthu zisanachitike. Iye sakanawapatsa iwo mwanayo ngati dzina lawo likanakhalabe chomwecho.

⁸⁵ Ndipo inu simungabadwe mwatsopano ngati dzina lanu mulibe mu Bukhu la Kumwamba. Inu mukhoza kuliyyika ilo pa mpingo uliwonse, Methodist, Baptist, Presbateria, kulinyamula ilo kuchokera kumalo kupita ku malo, kukangana ndi onse a iwo; koma ilo likuyenera kuyikidwa pa Bukhu la Kumwamba chirichonse chisanachitike, ndipo cholengedwa chatsopano chikhoza kubwera. Moyo watsopano usanabwere, mayina awo ankayenera kusinthidwa. Inu mungafune kusintha anu, inunso, kuchokera ku ena a mabukhu opangidwa ndi anthu awa, kupita ku Mabukhu a Kumwamba.

⁸⁶ “Ndipo pamenepo, dzina lako silinso *Abramu*, ‘atate wapamwamba; koma ndi *Abrahamu*, ‘atate wa mafuko.’ Osatinso (*Sarah*), *Sarai*, koma Sarah, ‘mfumukazi.’”

⁸⁷ Oh, apa ife tikubwera tsopano pa mutu wa 18. Kuyambira pa ya 17, tiyeni tipite molunjika ku ya 18, chifukwa ndi basi. . . Ine sindikufuna kuti ndipite kutali kwambiri ndi izo usikuuno, kuti ndikusungeni inu pano, chifukwa ine ndikufuna inu mudzabwerere mawa usiku. Tsopano zindikirani. Ndipo ife tifika, mwachangu momwe tingathere, pa ya 22. Penyani tsopano. Pamene izo zinafika tsiku lina, mwinamwake, titi, masiku awiri kapena atatu zitachitika izo, Abrahamu ndi Sarah, mahema awo anayikidwa.

⁸⁸ Kumusi mu mzinda kumusi uko, ine ndikulingalira Akazi a Loti anali atavala madiresi a mawonekedwe atsopano amene iwo anali nawo kumusi kumeneko. Ndipo iye ankakonzza tsitsi ndi chirichonse chimene iwo anali nacho. Iye ankangokhala moyo wawofuwofu, ndipo anali ndi ana ake aakazi onse chimodzimodzi basi. Momwemo basi momwe mayi hule

wachitira lero, ndipo wawapangitsa ana ake aakazi onse kuchita chinthu chomwecho.

⁸⁹ Tsopano, koma Sarah, komabe mkazi wokongola kwambiri mdziko lonse, anakhala pa dziko lowuma, chifukwa iye ankagwiritsitsa kwa iye amene anali ndi lonjezo. Tsopano ine kulibwino ndichokepo apa, chifukwa ine ndipita, ine ndi. . .Ndikusungani inu pano mpaka pakati pa usiku. Iye anagwiritsitsa kwa Abrahamu. Uko nkulondola. Iye anali ndi lonjezo.

⁹⁰ Gwiritsitsani kwa Khristu, Iye ndi Mmodzi amene ali ndi lonjezo! Iye ndi Lonjezo. Iye ndi Lonjezo! Zindikirani.

⁹¹ Tsiku lina dzuwa linatulukira lotentha kwambiri mmawa wina, Abrahamu anali atakhala kunja mu mthunzi wa hema wake uko pafupi ndi mthundu. Ndipo iye anayang'ana kumusi, kuyenera kuti inali pafupifupi leveni koloko, ndipo iye anawawona amuna atatu akubwera, akuyenda, fumbi pa zovala zawo. Ndipo Abrahamu anathamangira kumeneko. Munali chinachake mu mtima mwake chimene chinamupangitsa iye kumverera bwino kwenikweni, ndipo iye anathamangira kumeneko ndipo anagwa pansu pa mapazi awo. Ndipo penyani, iye anati, “Mbuye wanga!” Kodi izo sizachilendo? Atatu a iwo; koma “Mbuye wanga”!

⁹² Tayang'anani pa Loti. Pamene awiri a iwo anapita kumeneko, awiri okha a iwo, iye anati, “ambuye Anga.” Loti anawatchula iwo “ambuye.” Abrahamu. . .Loti anawatchula, awiri, “ambuye.”

⁹³ Ndipo Abrahamu anawatchula, atatu a iwo, “Mbuye! Mbuye wanga!” Amen! Oh, nthawi yayandikira! Zindikirani, iye anati, “Mbuye wanga, ngati ndapeza chisomo pamaso Panu, bwerani, mudzakhale pansu pa mthundu. Mundilole ine ndibweretse madzi pang'ono, ndi kusambitsa mapazi Anu, ndi kutenga chidutswa cha mkate. Pakuti ichi ndi chifukwa chokhacho chimene Inu mwabwerera, kudzandiwona ine.” Iwo anapita kumeneko.

⁹⁴ Iye anatuluka ndipo anapita kuseri kwa hema, ndipo anati, “Sarah, konza ufa mwachangu, ndipo upange mikate pa moto.” Anapita kumeneko ndipo anakatenga mwana wa ng'ombe, ndipo anamupha iye ndipo anamusenda, ndi kupanga nthulinthuli, ndipo anabweretsa batala ndi mkaka, ndipo—ndipo anaziyika izo pa mwamunayo, ndipo iwo anadya.

⁹⁵ Ndipo Mmodzi wa iwo anali Mulungu Mwiniwake! Ndicho chimene Baibulo linanena. Tsopano ngati inu mukufuna kutsutsana ndi Ilo, pitirirani nazo. Iye anamutcha Iye “Elohim, Mulungu.” Iye akuyenera kudziwa; iye ankayankhula ndi Iye. Zindikirani, “Ambuye Mulungu!” Tsopano, Mmodzi wa iwo anali Mulungu. Ndipo anayang'ana pa Iye. Abrahamu anazindikira izo. Tsopano yang'anani apo.

96 Mtumiki ananena ndi ine nthawi ina, iye anati, “M’bale Branham, inu simukutanthauza kundiuza ine kuti inu mumakhulupirira zimenezo, kuti Munthu ameneyo anali Mulungu?”

97 Ine ndinati, “Abrahamu anati Iye anali. Omasulira onse amasulira izo momwemo, chilemba chachikulu A-m-b-u-y-e. Ndipo aliyense amene amawerenga Baibulo amadziwa kuti chilemba chachikulu A-m-b-u-y-e ndi Elohim. Zimachokera ku mawu omwewo, Elohim! ‘Pachiyambi, pa chiyambi, Mulungu analenga,’ Elohim, Wamphamvuzonse, wopezeka Yekha, ‘analenga Miyamba ndi dziko lapansi.’ Ndi Uyo pamene kachiwiri, atayima patsogolo pake pomwe.”

Iye anati, “Chabwino, inu mukudziwa,” anati, “ameneyo—ameneyo anali munthu chabe.”

98 Ine ndinati, “Ndithudi, Iye anadya nyama, Iye anadya, kumwa mkaka, ndipo Iye—ndipo Iye—ndipo Iye anadya mkate.” Ine ndinati, “Ndithudi, Iye anali Mulungu.”

Iye anati, “Izo zikanatheka bwanji?”

Ine ndinati, “Bambo, inu—inu. . .”

99 Ine—ine ndikukhulupirira kuti izo sizikuvulaza kumverera kwanu; iwo anali a Mboni za Yehova. Ndipo iye anati kwa ine, iye anati, “Chabwino, Bambo Branham, tayang’anani apa, ine ndikufuna ndikuuzeni inu chinachake. Mulungu sangachite zimenezo.”

100 Ine ndinati, “Inu simukumudziwa basi Mulungu wanga. Ndizo zonse.” Ine ndinati, “Kodi thupi la munthu linapangidwa ndi chiyani? Petroliyamu, potashi, ndi kuwala kwadziko, zidutswa sikisitini. Chinthu chokhacho chimene Mulungu ankayenera kuchita ndi kutsika ndi kudzafufuza Sodomu, Iye anati. . . anangofikira ndi kumutengera Iye kuwala kwadziko kodzadza mdzanja ndi petroliyamu, ndipo ‘Psyii!’ Anati, ‘Bwera kuno, Gabrieli, lowa umu.’ Ndiko kulondola. Anafikira ndipo anatenga fumbi lina lodzaza mdzanja, ‘Bwera kuno, Mikaeli, lowa umu.’ Ndipo anadzipangira limodzi Yekha.” Iye ankayenera kuyimira chinachake chimene Iye ankati adzakhale mmasiku otsiriza, chotero Iye akubwera pansu pomwe ndi kudzayankhula mu thupi la munthu. Kulondola ndendende. Oh, ndine wokondwa kwambiri kuti Iye ndi wantundu umenewo!

101 Tsiku lina sipadzakhala kanthu kotsalira kwa ine. Ndine wopangidwa ndi zinthu sikisitini, nanenso. Ine ndinali kupesa tsitsi liwiri kapena litatu limene ndatsala nalo, tsiku lina. Mkazi wanga anandiyang’ana ine, ndipo anati, “Billy, iwe ukuyamba dazi.”

Ine ndinati, “Wokondedwa, ine sindinataye limodzi la ilo.”

Iye anati, “Iwe unali ndi tsitsi la mzindo.”

Ine ndinati, “Eya, koma sindinataye limodzi la ilo.”

Iye anati, “Ndikupempha kuti undiuze kumene ilo liri.”

¹⁰² Ine ndinati, “Ndiye, wokonedwa, iwe undiuze ine kumene ilo linachokera ine ndisanalipeze ilo. Ndipo kulikonse kumene ilo linali ine ndisanalipeze ilo, ilo liri kumeneko likudikirira kuti ine ndibwere kwa ilo.”

¹⁰³ Ameni! Ulemelero! Baibulo linati, “Palibe tsitsi limodzi la mmutu mwanu limene lidzawonongeka!” Aleluya! Ndiko kulondola ndendende. Izo sizinali, komabe ziri; ndipo komabe siziri, kenako ziri. Ndithudi. Ndendende! Petroliyamu, kuwala kwa dziko, kashiamu, potashi, ndi zina zotero. Mulungu... Pamene sindine kanthu, palibe chimene inu mungathe kuchiwona, phulusa basi, Iye adzayankhula, aleluya, kuponyera potashi ameneyo ndi petroliyamu pamodzi, ndipo ine ndidzakhhalanso moyo mu Kukhalapo Kwake. Aleluya! Iye amatipatsa ife Moyo Wamuyaya. Ameni. “Zonse zimene Atate andipatsa Ine, palibe chimene chatayika, ndipo Ine ndidzamuwukitsa iye kachiwiri mmasiku otsiriza.” Ine ndikukhulupirira izo! Monga Mbewu ya Abrahamu, ndikuyembekezera tsiku limenero! Ine ndikufunafuna Mzinda Umene Wowumanga ndi Wowupanga Wake ndi Mulungu. Ameni. Ndithudi. Ziribe kanthu momwe ili likupangira makwinya ndi kumakokeka, ndipo tsitsi kumathothokapo, ziribe kanthu chimene chingachitike, Mulungu adzaliwukitsa ilo kachiwiri, mu kukongola kwa unyamata kachiwiri, pa tsiku lotsiriza ilo. Iye analonjeza kuti Iye adzachita izo, ndipo ine ndikufunafuna Mzinda umenewo! Ameni. Oh, mai! Ine ndikumverera mwachipembedzo kwambiri pakali pano, podziwa, ndipo chiyembekezo chodalacho chikundiyeembekezera ine Kumeneko. Ine ndikufunafuna Mzinda umenewo. Mtima wanga ukugunda molunjika kwa Iwo. Oh, palibe njira imodzi imene ine ndingatembukire, koma kuyang’ana molunjika ku Malo amenewo. Mulungu, ndithandizeni ine kukhala pamenepo, woona ndi wokhulupirika, kuponya chingwe chamoyo, paliponse, ndi kumubweretsa mwendamnjira wotopa aliyense amene ine ndingathe, kuti apite nawo.

¹⁰⁴ Inde, ndinali ndi masomphenya a izo osati kale kwambiri, ndipo ndinaona izo, ndipo ndinawawona okonedwa anga kumeneko, atabwerera kukhala achinyamata kachiwiri. Ziri kumeneko. Ziri kumeneko. Ine ndikudziwa kuti izo ziriko! Inde, bwana! Tsopano, mwinamwake inu munaziwrenga izo mu *Christian Business Men’s Voice*, ndi magazini ambiri ndi zinthu zinalembe izo. Abwenzi, amenewo sanali masomphenya. Ine ndawonapo masomphenya, ine ndikudziwa, ndikuyenera kudziwa chimene iwo amakhala nazo, mwa ma teni ama sauzande zimene Iye amandipatsa ine. Koma awa sanali masomphenya. Ine ndinali pamenepo, nditayima pomwepo, ndikuyang’ana mmbuyo. Ndipo ndikudziwa kuti ziri kumeneko. Izo ziri kumeneko, abwenzi, ziri kumeneko! Ndikudziwa ziri

kumeneko! Inde bwana! Basi motsimikiza basi monga ine ndayima pano, chotero ndithandizeni ine, ngati ine ndiri ndi malingaliro anga abwino ndi kuyima pano pa guwa ili, izo ziri kumeneko! Mulungu anapanga lonjezo Lake, ndipo izo ndi zoono, ndi zoono! Inde, bwana. Ziri kumeneko. Zindikirani.

¹⁰⁵ Tsopano ife tikupeza kuti, amuna awa anakhala pansu ndi kumadya. Ndipo awiri a iwo ananyamuka ndipo anatsikira ku Sodomu. Mmodzi anatsalira ndi Abrahamu. Tiyeni tiwone zokambirana zawo. Iwo anapitiriza kuyang’ana cha ku Sodomu. Ndipo Abrahamu anadziwa kuti panali chinachake chachilendo pang’ono cha izo. Chotero Iye anati, kenako pamene Iye anakonzekera kuti azichoka, Iye anati, “Inu mukuganiza kuti ndimubisile Abrahamu; pokhala kuti iye adzakhala atate wa mafuko, ine ndikudziwa momwe iye ati adzalerere ana ake, zina zotero; chinthu chimene Ine nditi ndidzachite?” Iye anati, “Machimo a Sodomu ndi aakulu kwambiri mpaka alowa mmakutu Ake.” Iye anabwera pansu kuti adzafufuze.

¹⁰⁶ Tsopano kumbukirani, monga ine ndinanena usiku wina, awiri a atumiki amenewo anapita uko mu Sodomu, ndipo iwo anakalalikirira kwa aku Sodomu amenewo; ndipo iwo anawachititsa khungu iwo usiku umenewo, pa Mawu. Koma, kumbukirani, apo panali Mmodzi; iwo, iwo anali ndi chizindikiro chawo, Mlendo pakati pawo.

¹⁰⁷ Tayang’anani pa Loti. Loti atakhala pachipata, ndipo anati, “ambuye Anga.” Ndipo akukhala moteromo! Iwo anati, “Bwerani mnyumba yanga.” Iye anati, “Ife tigona mu msewu.” Ndi nyumba yotani!

¹⁰⁸ Koma mwamsanga pamene Abrahamu; iwo anati, “Ichi ndi cholinga chimene ife tadzera. Ife tikhala pansu apa pambali pako.”

¹⁰⁹ Ndiyo njira yake. Muzikhala chomwecho, kuti ngati Mulungu angafune kuti akugwiritseni ntchito, Iye azidziwa komwe angabwere nkudzakupezani inu. Inu muli pamalo, mukukhala moyo woyera pamaso pa Mulungu, mawu anu ndi owona, moyo wanu ndi wona. Umenewo ndi mtundu wa malo amene Angelo amabwerako. Tayang’anani pa—pa Elizabeti ndi Zakariya, mwaona, owongoka owonamtima, akuyenda mu Malamulo onse a Ambuye. Umo ndi momwe ife timafunira kukhalira moyo, chotero pamene Mulungu wakonzeka kuti atigwiritse ife ntchito, Iye amati, “Awa ndi anthu Anga. Ine ndikhoza kuchita ndi mpingo uno chimene Ine ndikufuna. Iwo amandikhulupirira Ine. Iwo amayima pa Mawu Anga.” Mwaona, umo ndi momwe inu mumafuna kuti muzichitira, kukhala moyo.

¹¹⁰ Tsopano ife tikupeza kuti Mngelo uyu, Iye anati, “Ine sindimubisira Abrahamu. Koma ndidzakuchezera iwe molingana ndi nthawi ya moyo.” Ndipo, zindikirani, Iye sanamutche iye *Abramu*, Iye anamutcha iye “Abrahamu.” Kodi

Iye anadziwa bwanji kuti dzina limenero linali litasinthidwa? Iye anali Amene analisintha ilo. Ndithudi. Zindikirani, sanamutchule konse *Sarai*, inu mukudziwa, S-a-r-a-i. S-a-r-a-h, “Ali kuti mkazi wako, Sarah?” Kodi Iye anadziwa bwanji kuti iye anali wokwatira? Kodi Iye anadziwa bwanji kuti iye anali ndi mkazi, ndipo dzina lake linali Sarah?

Ndipo Abrahamu anati, “Iye ali mu hema kumbuyo Kwanu.” Dona weniweni bwanji!

¹¹¹ Lero, akazi amakhala aphokoso kwambiri! Aliyense... Mwamuna wawo amalephera kuti ayankhule. Iwo amayenera kukakamira pamenepo, ndudu mdzanja lawo, atavala akabudula, akupanga kuyankhula konse. Ndi mtundu wopotozedwa bwanji wa anthu, iye akuyenera kukhala wophika wamkulu ndi wotsuka mabotolo, china chirichonse! Akachoka ku khitchini, iye akusiya malo ake a ntchito, kulondola, monga mayi.

¹¹² Tsopano ife tikupeza kuti, akazi kalelo ankakhala kuseri ndi kumakhala akhalidwe, kumachita monga madona, mutu wawo unali amene ankapanga ziganizo ndi zinthu.

¹¹³ Ndipo inu muyesere kumulola mwamuna wina kuti amuuze mkazi wake; iye amati, “Ndikupatsa iwe kuti umvetse pompano!” Psyii! Psyii! Akutulutsa utsi umenewo kuchokera mkamwa mwake, akuyang’ana chomwecho, mawonekedwe owopsya. Ine sindinaziwonapo zoterozo! Ndipo inu mukhoza kulingalira kunjira uko, ndi kuyima pamenepo kumamuyang’ana munthu ameneyo, kuwuzindikira mzimu umenewo mmenemo, ndi zinthu zimenezo; ndipo mwinamwake woyimba mu kwaya mu tchalitchi china. Oh, tsiku lotere limene ife tikukhalamo! Nzosadabwitsa ife tiri pa tsiku limenero! Ine—ine ndikukhulupirira kuti mukumvetsetsa kudutsa pa lanya chimene ine ndikutanthauza.

¹¹⁴ Zindikirani, izo zinali pamenepo. Sarah anali mu hema, iye anali ali mmenemo ndipo iye anali wakhalidwe. Abrahamu ankapanga kuchereza Angelo awa. Tsopano, ndipo Iye anati, “Ine ndidzakuchezera iwe.”

¹¹⁵ Ndipo Sarah anali akumvetsera. Ndipo anaseka chamseri, iye anati, “Ine, mkazi wokalamba, wokalamba momwe ndiliri, ndipo apo mbuye wanga wokalambanso, ndipo kunena kuti tidzakhalanso ndi chisangalalo monga mwamuna ndi mkazi?” Ndipo iye anaseka.

¹¹⁶ Ndipo Mngeloyo, nsana Wake atawutembenuza, anati, “Nchifukwa chiyani Sarah anaseka?”

¹¹⁷ Kumbukirani, chimenecho chinali chizindikiro chotsiriza chimene Mbewu ya... kapena Abrahamu mwiniwake, amene ali choyimira cha Mpingo, chinali chizindikiro chomaliza chimene iye analandira. Kuchokera ku zizindikiro zina zonse

zimene iye analandira, chimenecho chinali chomaliza Sodomu asanawonongedwe. Uko nkulondola? Chizindikiro chomaliza!

118 Pamene Israeli, mbewu imene inamutsatira Abrahamu. Ndipo Asamaria, amene anali mbewu yotayika ya mtundu wosakanizika, akumufunafuna Iye, chonchobe; iwo anati, “Athu—atate athu Yakobo anatipatsa ife chitsime ichi,” mkaziyo anatero ku Sukari. Mukuona? “Atate athu Yakobo, iye—iye anapereka chitsime ichi kwa Yosefe, mwana wake, ndipo—ndipo takhala tikumwa kuchokera kwa icho, ndipo iye anamwetsa ngamira zake. Ndipo Inu mukuti Inu muli ndi madzi, zina zotero monga choncho?” Mukuona? Ndipo chizindikiro chotsiriza chimene mbewu ya Israeli, mwachibadwa, inachilandira, chinali chizindikiro cha mtundu womwewo! Psyii! Kodi simukuziwona zimenezo? Taganizani miniti!

119 Chizindikiro chotsiriza chimene Abrahamu ali ndi pangano, chizindikiro chotsiriza mpingo wofunda usanakanidwe, ndi chiwonongeko chake, chinali chizindikiro chozindikira maganizo a mmitima ndi maganizo, Mulungu anawonetseredwa mu thupi la munthu.

120 Ndipo chizindikiro chotsiriza chimene Israeli anachiwona iye asanadulidwe, chinali chinthu chomwecho. Ndipo iwo anati, “Ndi Bezebule; wam’bwebwe.”

121 Tsopano ndiro oralo! Mulungu, mulole izi zilowe mkati! Tsopano ndi oralo, limene, Mbewu yachifumu ya Abrahamu! Kodi mukumvetsa zimenezo? Mulungu anawonetseredwa mu thupi la munthu, kuwapatsa iwo chizindikiro chawo chotsiriza chiwonongeko cha ofunda chisanachitike ndi kupita monga zinachitikira. Womaliza! Ulemelero womaliza wa kubwerera mmbuyo kwa Loti! Mulole izo zilowe miniti yokha.

122 Abrahamu, yoyamba; mbewu yachirengedwe ya Abrahamu, yachiwiri; Mbewu yachifumu ya Abrahamu, yachitatu.

123 Penyani, Uthenga sumatenga ofunda kunja uko. Nkuti kumene Iwo unapita nkomwe kwa iwo? Unatumizidwa kwa achipentekoste, osankhidwa, otulutsidwa-atuluke.

124 Ndipo monga Israeli anachitira nthawi imeneyo, nainte- . . . Penyani ndi angati, penyani ndi a Israeli angati anawulandira Iwo. Pamene nthawi inafika yoti iwo apite kumeneko, apo panali handirede ndi twente mwa pafupifupi foro milioni.

125 Tsopano penyani Mbewu yachifumu. Mwaona, iyo ikuyenera kubwera nthawi zitatatu zimenezo, mwaona, kulikonse kumene inu mungatenge. Anthu a Hamu, Shemu, ndi Yafeti. Mbewu yachifumu ya Abrahamu! Pali Abrahamu; mbewu yathupi; Mbewu yachifumu. Chirichonse! Mbewu yachifumu ili mwa Khristu, kudzera. . . Ife tikubwera ku lonjezo la Abrahamu limene Mulungu anamupatsa iye kudzera mwa Khristu, Mbewu yachifumu. Ndipo iyi ndi Mbewu yachifumu, Mpingo uwu wa Ambuye Yesu umene Iye akuwubwezeretsa mmasiku

otsiriza. Mbewu yachifumu! Zindikirani, iye analandira chizindikiro chimenecho! Ndipo Mbewu yachifumu Iyemwini anati, pamene Iye anali kuno, “Monga izo zinali mmasiku a Loti, chomwechonso izo zidzakhala mu kudza kwa Mwana wa munthu.” Mbewu yachifumu, Mbewu ya Abrahamu, yoyitanidwa ituluke; Loti nayenso, wa m’bale wake, wofunda, uko ku Sodomu; ndipo kenako waku Sodomu, dzikolo. Lero, dziko; mpingo wa dziko; ndi Mbewu yachifumu. Ndendende, iwo akukhala mwapamalo ndi chirichonse, ndendende basi molingana ndi dongosolo. Ndipo Mulungu, ndi lonjezo Lake, wabwera pansu pomwe, kudzawonetsera chinthu chomwecho. Amen. Ngati icho si changwiwo, ine sindikudziwa kuti ungwiro ndi chiyani. Ndi Malemba!

¹²⁶ Inu mwakhalapo nako kuyankhula mmalirime, kuvina mu Mzimu. Inu mwakhalapo nazo zogirigisha zonse izi zimene inu munali nazo, mwaonapo zozizwitsa za machiritso, ndi—ndi zikuku, ndi zina zotero. Ife taziwonapo zonse za izo. Koma apa, apa pali chizindikiro chomaliza chimene chabwera tsopano. Abrahamu anawona mitundu yonse ya zinthu zimene Mulungu anamuchitira iye panjira, ndithudi, koma apa pakubwera chizindikiro chotsiriza, mwana wolonjezedwayo asanabwere. Ndipo tsopano Mbewu yachifumu ikufunafuna Mwana wolonjezedwa. Aleluya! Kodi ife, kodi ife tikuyang’anira Mwana wolonjezedwayo? Mwana wa Mulungu kuti abwera! Aleluya! Oh, izo zikundipangitsa ine kumverera ngati ndifuule. Penyani! Mbewu yachifumu ikuyembekezera Mwana wolonjezedwa. Monga Abrahamu anachitira kudutsa mzaka, kuyang’ana, akugwiritsitsa ku Mawu amenewo, chomwechonso Mbewu yachifumu yatero. Ndipo Mbewu ikuyang’anira Mwana wakudza uyu, kudza kwa Ambuye, kupyolera mu ulonda umodzi, ulonda uwiri, ulonda utatu, mpaka ku ulonda wachisanu ndi chiwiri, ndipo pano ife tikuyang’anirabe Mbewu yachifumu. Ndipo kodi ife tikuwona chiyani Kudza kwa Ambuye kusanachitike? Chikuchitika ndi chiyani? Mulungu akutsika pakati pathu, kudzawonetsera Mbewu yachifumu monga Iye anachitira mbewu ya Abrahamu; ndipo Abrahamu, ndi mbewu ya Abrahamu, ndipo apa Izo ziri ndi Mbewu yachifumu. Mulungu akukhala pakati pathu mu mawonekedwe a Mzimu Woyera, akuchita zinthu zomwezo zimene Iye ankazichita kumbuyo uko, kumachita, kumawonetsera kuti ndi zofanana.

Ndipo pa kafukufuku wa sayansi pa chithunzichi, dziko likudziwa, dziko la sayansi likudziwa kuti ndi zoon.

Mpingo ukudziwa kuti izo ndi zoon, dziko lonse.

¹²⁷ Ndipo ine ndikukhulupirira kuti Mbewu yokonzedweratu iliyonse ili pafupi kulowa, chitseko chatsala pang’ono kutsekedwa, ndipo chiweruzo chiri pafupi kuti chikanthe. Uko nkulondola. Mulungu nthawizonse sadzalimbana ndi

munthu. Iye adzachita chirichonse chimene Iye angathe. Koma oralo likuyandikira, abwenzi. Zindikirani.

¹²⁸ Ine ndikupatsani inu chinachake kuti chikuthandizireni inu tsopano. Kumbukirani, chinthu chotsatira chimene chinachitika chinali chiyani tsopano? Iwo asanalandire mbewu yachifumu, pankayenera kuchitika chozizwitsa kwa awiri onse Abrahamu ndi Sarah, mwathupi, pasanakhale mbewu yachifumu. . . kapena mbewuyo isanabadwe. “Tsopano, thupi la Abrahamu linali ngati lakufa,” Baibulo limanena zimenezo. Sichoncho izo? “Ndipo chiberekero cha Sarah chinali chakufa,” Baibulo linanena chomwecho. Tsopano pankayenera kukhala chinachake chathupi chikuchitika mbewu yachifumu isanakhale. . . mbewuyo isanawonekere mwana wolonjezedwayo. Mwana wolonjezedwayo asanawonekere, pankayenera kuti pakhale chinachake chathupi chikuchitika mu thupi lawo, mwana wolonjezedwayo asanawonekere. Penyani chimene Iye anachita. Ine ndikupatsani inu chinachake chaching’ono.

¹²⁹ Tsopano, kuweringa Baibulo, Iyo ndi Nkhani yachikondi imene Mulungu analemba ku Mpingo Wake. Ndi Mulungu. Mulungu ndi chikondi. Kodi inu mukukhulupirira zimenezo? Ndipo Baibulo linalembedwa kuchitira kuti ophunzira ndi anzeru asadzathe konse kulimvetisa Ilo. Inu mukuyenera kukhala mu chikondi ndi Mulungu kuti mulimvetse Ilo. Inu mukuyenera kukhala ndi Mulungu mwa inu. Iye amadzitanthauzira Yekha kwa inu.

¹³⁰ Tsopano, izo ziri ngati ine ndiri ndi mkazi. Oh, momwe ine ndimamukondera iye! Ine ndimamukonda iye ndi mtima wanga wonse. Ndipo ndikakhala kutsidya kwa nyanja kwinakwake ndipo iye. . . iye akawagoneka ana, amandilemba kalata, ndikuti, “Wokonedwa Billy, ine ndakhala pano usikuuno, ine ndikuganiza za iwe. Ndikulemba.” Mwaona, ine ndikudziwa chimene iye akulemba pa pepapalapo. Koma ine ndimamudziwa iye ndipo ndimamukonda iye kwambiri mpaka ndimadziwa chikhalidwe chake, ine ndimadziwa chimene iye amatanthauza, chotero nditha kuweringa pakati pa mizere. Mukuona?

¹³¹ Ndipo Mulungu akufuna kuti Mpingo Wake uziweringa pakati pa mizere. Osati kuweringa *chirichonse* kuchokera mwa Iwo tsopano! Inu mukuyenera kuweringa pakati pa mizere kuti muwone tanthauzo lake. Tsopano penyani ndipo muwone, mupeze ngati Iwo sakutero.

¹³² Tsopano, chimene Mulungu anachita ndi Abrahamu ndi Sarah, Iye akuwawonetsa iwo, chitsanzo cha Mpingo Wake. Iye anawachitira iwo, Iye anawasintha iwo awiri onsewo kuti adzakhale mnyamata ndi mtsikana. Ndithudi, Iye anatero, anawabwezeranso iwo kukhala achichepere kachiwiri, chimodzimidzi monga momwe Iye ati adzachitire

kwa Mbewu iliyonse ya Abrahamu. Ziribe kanthu kuti ndinu wamkulu bwanji ndi wosweka mtima, pakubwera tsiku limene mudzakhala wachinyamata ndi wokongola kenanso, uko nkulondola, ulemelero wa moyo.

¹³³ Ine ndinamufunsa dokotala osati kale, “Ndiuzeni ine, bwana. Nthawi iliyonse ndikadya, ndimatsitsimutsa moyo wanga.”

Iye anati, “Inde, bwana, izo nzoona.”

¹³⁴ Ine ndinati, “Tsopano, Mulungu ananena kuti ife ‘tinapangidwa kuchokera ku fumbi la mnthaka.’”

¹³⁵ Iye anati, “Izo nzoona. Masamba ndi nyama ndi zinthu zimene mumadya ndi fumbi. Kumene inu mumapeza potashi ndi kashiamu wanu ndi zinthu mu mavitamini anu, inu kenako mumazibweretsa izo kuchokera mnthaka. Ndipo inu munapangidwa kuchokera ku fumbi lapansi.”

Ine ndinati, “Hum. Tsopano, Mulungu analenga ilo poyamba monga choncho.”

¹³⁶ Iye anati, “Ine sindikudziwa kanthu za izo, koma” anati “Ine ndimadziwa ndiye kuti tsopano umadya chakudya ndipo icho chimamanga thupi lako.”

¹³⁷ Ine ndinati, “Ndikukufunsani inu.” Ine ndinati, “Ndiye inu mukundifunsa ine za kubadwa mwa namwali?”

Iye anati, “Inde, bwana, ndikutero.”

¹³⁸ Ine ndinati, “Ndikufuna ndikufunseni inu chinachake, adokotala. Mufotokeze izi kwa ine.”

¹³⁹ Iye anati, “Chabwino, chirichonse chimene sichingatsimikiziridwe mwasayansi sicholondola.”

¹⁴⁰ Ine ndinati, “Ine nditenga mbali yotsutsa, kuti chirichonse chotsimikiziridwa mwasayansi sichiri choncho, palibe kanthu kwa icho.” Ndipo ine ndinati, “Zinthu zenizeni zokhazo zimene ziripo mmoyo ndi zinthu zimene sizingatsimikizidwe mwasayansi: chikondi, chimwemwe, mtendere, kuleza mtima, chifatso, chipiro, chikhulupiro. Mwasayansi munditsimikizire izo kwa ine? Komabe ndi zenizeni! Mulungu, Mzimu Woyera, Angelo!” Ameni! “Chikhulupiro chimachita zinthu zimenezo. Chirichonse chimene inu mumachiwona ndi chochokera pa dziko lapansi, chinachokera kwa manthu dziko lapansi, chikubwerera njira yomweyo.” Ine ndinati, “Ine ndikufuna ndikufunseni inu chinachake. Pamene ndinali ndi zaka sikisitini, ndinkadya chakudya chomwecho chimene ndikudya pakali pano. Ine ndinkadya nyemba, mbatata, ndi buledi, ndi nyama. Ndipo nthawi iliyonse ndikadya, ndinkakula ndi kukhala wamphamvu.”

Iye anati, “Ndithudi, inu munkatsitsimutsa moyo wanu.”

¹⁴¹ Ine ndinati, “Nchifukwa chiyani, nditadutsa pafupifupi zaka twente thuu zakubadwa, wina aliyense, ziribe kanthu kuti ukudya mochuluka bwanji, umafookabe ndi kukalamba? Taganizani za zimenezo.” Ine ndinati, “Ine ndiri jagi ya madzi apa, ndipo ndiri ndi galasi; ndipo ine ndinayamba kuthira madzi mu jagi yaikulu iyi mu galasi ili, ndipo inayamba kudzaza mpaka inadzaza theka; ndiyeno wopanda kalikonse pansi apa nkomwe, pamene ine ndimatsanulira mochuluka, ndi pamene iwo amapita pansi. Ziribe kanthu momwe ine ndimadyera mochuluka, mwabwino bwanji; ndimadya bwinoko tsopano kuposa momwe ndinkachitira, kuchulukitsa ka handired.”

¹⁴² Ndikudziwa chimene chinali kutafuna zikopa za nyama usiku wonse, ndikudya mkate wa chimanga ngati kadzutsa ndi manyuchi a mapira, ndipo chinthu chomwecho pa chakudya chamadzulo ndi mgonero, aponso. Ndikudziwa chimene icho chinali kukhala moyo wovuta, ndipo tsopano nditha kudya bwinoko. Zikomo Ambuye. Koma ngakhale ndidye mochuluka bwanji, ndikufookabe ndi kukalamba. Ndipo pamapeto pake ndidzauma ndi kufa. Bwanji? Bwanji? Ndi nthawi imene Mulungu wayipanga. Uko nkulondola. Inde, bwana.

¹⁴³ Ndipo zindikirani Abrahamu ndi Sarah, iwo anabwerera mmbuyo ku pafupifupi usinkhu wa zaka twente-thuu kapena twente-faivi.

¹⁴⁴ Oh, inu mukuti, “Zamkutu, M’bale Branham!” Chabwino, tsopano khalani bata miniti yokha, tiyeni tingowerenga pakati pa mizere kamodzi.

¹⁴⁵ Angelowo atangochoka, ndipo Sodomu anatentedwa, Abrahamu ndi Sarah anayenda ulendo wautali mpaka ku Gerari. Uwu ndi ulendo wautali kwa banja lokalamba. Muwuyeze pa mapu anu. Iwo anapita kumusi ku Gerari. Ndipo apa pali Sarah tsopano, agogo aakazi, usinkhu wa zaka nainte, atavala kachipewa kakang’ono ka dzuwa, akunjenjemera. Ndipo Abrahamu ndi ndevu zake zazitali zikulendewera pansi. Baibulo linati, “Onse awiri anali okalamba kwambiri.” Sindikuyesera kunena kuti anakhala nthawi yayitali. Ndipo Baibulo linati, “Matupi awo onse awiri anali akufa, okalamba kwambiri.” Ndipo apa iwo akupita ku Gerari. Ndipo kunali mfumu yang’ono kumusi uko yotchedwa Abimeleki, ndipo iye ankafunafuna womukonda, ndipo pamene iye anamuwona Sarah anamukonda iye. Nkulondola uko? Agogo aakazi?

¹⁴⁶ “Bwanji, ndiwe wopambana!” Abrahamu anati, “Ndiwe wokongola kukuyang’ana.” Amen. “Ine ndikukupempha iwe, umuuzi iye kuti ndiwe wanga—mlongo wanga.” Aleluya! Iye ankawonetsera pamenepo chimene Iye akanati adzachitire Mbewu yonse ya Abrahamu. Sarah anali wokongola. Abrahamu anali wamng’ono. Ine ndikukhoza kumumva Abrahamu akuti,

“Sarah, wokonedwa, ukudziwa chiyani, imvi zikuchoka mu tsitsi lako.”

147 “Abrahamu, linunda likuchoka pa nsana pako. Iwe ukuwongoka.” Iwo anabwerera kudzakhala mnyamata ndi mtsikana. Mulungu, akuwonetsera! Oh, mai!

148 Ndipo Abimeleki anamukonda iye, ndipo anapita ndi kukamutenga iye, akanamukwatira iye. Ine ndikukhoza kumuwona iye akusamba, ndi kugona pansu atavala zovala zake zogonera, ndi kukweza zala zake mmwamba, iye atatha kunena mapemphero ake, ndipo anati, “Mawa ndimukwatira wokongola wa zaka handirede ameneyo”? Zopusa! “Mtsikana wokongola wa Chihebri uja! Oh, mchimwene wake, mnyamata wamng’ono uja! Ndipo iye ndi wokongola bwanji!”

149 Ndipo Mulungu anawonekera kwa iye mu loto, ndipo anati, “Ndiwe basi ngati munthu wakufa.”

Anati, “Ambuye, chifukwa chiyani?”

Iye anati, “Ameneyo ndi mkazi wa munthu.”

150 Iye anati, “Inu mukudziwa ungwiro wa mtima wanga, Ambuye. Iye anati, ‘Ameneyo ndi mchimwene wanga.’ Ndipo iye anati, ‘Ndi mlongo wanga.’”

151 Iye anati, “Inde, ndikudziwa ungwiro wa mtima wako, ndi chifukwa chake Ine ndakuletsa iwe kuti usandichimwire Ine.” Koma mvetserani! “Koma iwe uli ngati wakufa, ndipo fuko lako lonse lapita. Mwamuna wake ndi mneneri Wanga. Ine sindikusamala momwe iwe uliri woyera, momwe iwe umapempherera, ine sindimva mapemphero ako. Koma mwamuna wake ndi mneneri! Pita, ndipo ukamubwezere mkazi wake ndipo umulole iye akupempherere iwe. Ngati iwe sutero, iwe ufa.” Aleluya!

152 Kodi chinali chiyani chimenecho? Mulungu kumukonzekeretsa Sarah ndi Abrahamu kuti alandire mwana wolonjezedwayo. Kuwonetsera kuti chinthu chotsatira pambuyo pa mawonetseredwe a Mngelo wa Mulungu uyu, Mzimu Woyera ukusonyeza chizindikiro Chake chotsiriza, chinthu chotsatira, chachivundi ichi chidzatenga chisavundi ndipo tidzakwatulidwa kupita mu mlengalenga kukakomana ndi Mwana wolonjezedwa, Mbewu yachifumu ya Abrahamu. Ulemelero kwa Mulungu! Aleluya! “Pakuti ife tidzasandulika mkamphindi, mu kuthwanima kwa diso, ndipo tidzakwatulidwa pamodzi kukakomana ndi Iye mu mlengalenga. Chotero ife tidzakhala nthawizonse ndi Iye, Mwana wolonjezedwa.” Aleluya!

153 Oh, ine sinditenga. . . Ine ndi. . . Mwinamwake mawa usiku ndidzatenga mutu wa 22, mwaona.

154 Oh, ndimazikonda izi, sichoncho inu? Ndine wokondwa kwambiri, zinthu zonsezi! Baibulo ndi lodzaza ndi zidutswa

zachisomo izi. Ingofikirani pansi ndi kutola izo, kuchotsa fumbi pa izo ndi kuziyang'ana izo. Aliyense wa iwo amaimira Yesu Khristu, munthu aliyense, pakuti mwa Iye munkakhala chidzalo cha Mulungu. Mwa Iye, chirichonse chimalozako. Chirichonse kuyambira ku Chipangano Chakale chimalozera ku mtanda; ndipo chiri mu Chipangano Chatsopano, chimaloza ku mtanda. Uko nkulondola. Zonse ziri mmenemo. Oh!

Chodala chikhale chimango chomwe
chimamangiriza
Mitima yathu mu chikondi cha Chikhristu;
Chiyanjano cha malingaliro apaubale
Chiri chonga chiya Chakumwamba.

¹⁵⁵ Momwe ine ndimamkondera Iye! Momwe ine ndikufunira kumuwona Iye! Momwe ndimayembekezera ndi kudikirira thupi lomenyedwa lakale ili, lovulazidwa, losweka mtima, lophwanyika kuti lidzasinthidwe limodzi la mmawa uwu! Lipenga lidzalira ndipo akufa mwa Khristu adzauka. Ife tidzakwatulidwira mmwamba ndi iwo, kukakomana ndi Ambuye mu mlengalenga.

¹⁵⁶ Momwe Rebekah anamwetsera ngamila ija mu kuzizira kwa madzulo. Elieza sanamupeze iye mmawa. Iye sanamupeze iye masana; anamupeza iye mu kuwala kwa madzulo. “Kudzakhala Kuwala mu nthawi ya kumadzulo!” Kulondola! Ndi kumene iye anamupeza iye. Iye anaphimba nkhope yake. Iye analibe mutu; iye anali akupita ku mutu wake. Amen. Mkazi, ndi chikhhalidwe chake, cha mkazi, kuti adzipereke kwa mwamuna. Ndipo ndi chikhhalidwe cha mpingo kudzipereka kwa Khristu, kudzipereka ku chifuniro Chake. Kungodzipereka! Iye alibe kuganiza kwake kwake; iye amatenga Mawu Ake, osati a winawake. Ngati Eva akanachita zimenezo, sitikanayenera kuti tizifa; koma iye anamvetsera ku kulingalira. Koma Mkwatibwi weniweni wa Khristu amatenga Umutu wa Khristu, Mawu, ndipo amangokhulupirira Mawu a Mulungu. Ameneyo ndi weniweni, Mkwatibwi wobwezeretsedwa. Aleluya! Nthawi yatsala pang'ono, abwenzi, nthawi yatha kuposa momwe mukuganizira. Ife tiri mu nthawi ya kumadzulo. Mzimu Woyera uli pano usikuuno. Ine ndikudziwa kuti ndi kagulu kakang'ono, kapang'ono.

¹⁵⁷ Inu mukhoza kuganiza, “Oh, ngati chinachake chonga icho chingachitike, Mulungu angakachiwonetsere icho mu Roma, kwa mabishopu ndi kwa mapapa. Iye angabwere kwa bishopu wa Methodisti. Iye angapite ku seminare ya Baptisti. Iye anga. . .” Eya, ndi chimene inu mukuganiza. Koma Iye sanachite konse izo mwanjira imeneyo.

¹⁵⁸ Iye amabwera kwa mtima wodzichepetsa, iwo amene akumuyembekezera Iye. Ndipo apa Iye ali usikuuno, Mzimu Woyera, Mulungu, Mngelo yemweyo; apa pamaso

pa asayansi, kutsimikizira, ndi Uyo apo ndi chithunzi Chake chitajambulidwa. George J. Lacy, wamkulu wa zodinda zala ndi mapepala wa FBI, iye anati, “Kuwalako kunakhudza magalasiwo.” Iye anati, “Bambo Branham, ine ndanenapo nthawi zambiri kuti kunali kuwerenga maganizo, kuti inu mumawerenga maganizo a anthu amenewo. Koma” anati “diso lamakina la kamera iyi silingatenge kuwerenga malingaliro. Kuwalako kunakhudza masowo. Izo zinali pamenepo!” Ndi Icho apo. Chimodzi cha izo chinapachikidwa ku Washington, DC, ufulu wotetezeka, “Chokhalapo chauzimu chokhacho chimene chinajambulidwa mwasayansi ndi kutsimikiziridwa.”

¹⁵⁹ Chifukwa chiyani? Ngati ine ndingafe usikuuno, ngati ine sindidzalowanso pa guwa ili mawa usiku, mawu anga ndi Choonadi. Chifukwa, si mawu anga, ndi Ake. Ine sindinanenepo “ndekha.” Si ineyo. Ine sindinathe kuchita kanthu. Ndine munthu ngati inu, wochimwa wopulumutsidwa mwachisomo. Koma Mulungu, mmasiku otsiriza ano, analonjeza zinthu izi, ndipo ndi izi apa! Ndi Mawu. Ngati izo zinali zopeka zina, zikhoza kukhala zosiyana. Koma ndi Mawu akutsimikizira Mawu mwa Mawu, kutsimikiziridwa, kudzera Baibulo. Zotsimikiziridwa ndi asayansi! Kutsimikiziridwa ndi Mzimu! Kutsimikiziridwa ndi mpingo! Mulungu pakati pathu! Aleluya. Ndine wokondwa kwambiri ndi zimenezo. Kodi sindinu okondwa, usiku watha, inu munayima ndipo munapanga kuyima kumeneko? Kodi izo zinakupangitsani inu kumverera mosiyana? Izo nthawizonse zidzatero, pamene inu muyima ndi Mawu a Mulungu. Kumuimira Khristu! Osachita manyazi ndi Zimenezo.

Tiyeni tipemphere.

¹⁶⁰ Kodi alipo aliyense muno usikuuno amene angafune kukweza dzanja lanu kwa mphindi chabe tsopano, ndi kuti, “M’bale Branham, ndikumbukireni ine mu pemphero lanu. Ine nditero, ine ndikufuna kwambiri kukhala mmodzi wa Mbewu izo za Abrahamu. Ine—ine sindikufuna ndidzaphonye Kumwamba. Pempherani, M’bale Branham. Nthawizonse pansu mu mtima mwanga ndimamverera ngati pali chinachake chimene ndachifikira. Ine sindinathe kuchipeza icho. Ndipemphererereni ine, M’bale Branham, kuti Mulungu apereke icho kwa ine?” Mulungu akudalitseni inu. Tangoyang’anani pa manja, paliponse, akubwera mmwamba.

¹⁶¹ Nanga bwanji mkhondemo? Tsopano, kumbukirani, Mulungu ndi wamkulu basi mu khondemo monga Iye ali pansu pano.

¹⁶² Kodi ndinu woona mtima kwenikweni, mukutanthauza izo? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Mulungu akudalitseni inu. Ine ndikungoyang’anira kanthawi. Muzingopemphera, mitu yanu ikhale yoweramitsidwa.

163 Wochimwa muno usikuuno angafune kukweza dzanja lake, kunena, “Ndikumbukireni ine, Ambuye. Ine sindikukwezera dzanja langa kwa mlaliki ameneyo; ine ndikukweza dzanja langa kwa Inu. Ine ndikukhulupirira moona kuti Inu muli moyo lero, kuti Inu simunafe konse; kuti pamene Inu munafa, Inu munauka kachiwiri, kani. Ndipo Ndinu wamoyo kwanthawizonse, yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ine ndikukweza dzanja langa kwa Inu, chifukwa ine ndikukhulupirira Inu muli pano?” Kwezani dzanja lanu, nenani, “Ndikumbukireni ine, Ambuye.” Muzingopemphera. Khalani ndi chikhulupiro mwa Mulungu.

Wobwerera mmbuyo, ndiye? Mulungu akudalitseni inu. Iye akuwona manja anu.

164 Atate athu Akumwamba, Inu mukuwona manja amenewo. Mukudziwa chimene chiri kumbuyo kwawo. Inu munati, “Wofesa anapita kukafesa Mbewu. Ina inagwera m’mphepete mwa njira, siinachite ubwino uliwonse; ina inagwera pamiyala; ina paminga; ina inalowa mu mahandirede.” Wofesayo anali kokha ndi udindo wofesa Mbewu. Mulole Mzimu Woyera uyigwire Mbewu imeneyo pakali pano. Ambuye, ife . . . Ine—ine ndikukhulupirira, Ambuye, ife . . .

165 Palibe munthu amene akudziwa pamene Inu mukubwera. Ife sitikudziwa izo. Inu munati, “Osati ngakhale Angelo angadziwe; Atate okha.” Yesu anadzinenera kuti Iye samadziwa. “Atate okha.”

166 Tsopano, Atate, ine ndikupemphera kuti ngati alipo muno amene anakweza manja awo, ine ndikukhulupirira iwo amatanthauza zimenezo. Pali Chinachake kumbuyo kwawo, chimene, Mzimu, umene unawauza iwo kuti akweze manja awo, ndipo iwo anachita izo. Iwo ndi owona mtima. Mwinamwake iyi ndi nthawi yoyamba imene Inu munayamba mwayankhulanapo ndi iwo, ndipo ikhoza kukhala nthawi yotsiriza. Mwinamwake Inu munayankhula nthawi zina, ndipo simudzayankhulanso. Ine sindikudziwa. Koma, Atate Akumwamba, ine ndikupemphera kuti Inu mupereke chipulumutso kwa aliyense amene akukhulupirira.

167 Mulole Dzina Lanu Loyera libweretsedwe molemekeza pamaso pa anthu. Mulole chikondi Chanu chitsanuliridwire kunja mu mtima uliwonse ndi Mzimu Woyera. Adalitseni abale otumikira awa, Ambuye. Amuna ofunika awa pano amene ali, mkati mwa mkangano, iwo anandiyitana ine, mulimonse. Adalitseni anthu amene abwera.

168 Ine sindikutanthauza kuti ndikhale wodzikuzwa, ine sindikutanthauza kuti ndikhale wosiyana, Ambuye; moona basi. Ndipo ndicho chinthu chokhacho chimene Inu muti muchizindikire, ndi choonadi chimene chiri mwa munthu, pakuti Inu ndi Choonadi. Invani tsopano, Atate, ine

ndikupemphera. Perekani kwa iwo usikuuno kuti ambiri a iwo pano, amene mwina sanakweze manja awo, apulumutsidwe, mulimonse. Perekani izi, mu Dzina la Yesu. Amen.

¹⁶⁹ Tsopano pamene ife takhala molemekeza mphindi yokha. Ine ndikukhulupirira ife tangochedwa pang'ono kuti tikhale ndi mzere wa pemphero, koma ife tikhala nawo. Munthu aliyense, pamene inu...inu, ngati inu muli ndi khadi, inu mugwire khadi lanu. Ngati mulibe khadi, mupeze imodzi. Ndife...Ngati ife tingakhale pano masiku faivi owonjezera, ife tipempherera aliyense wa iwo. Uko nkulondola.

¹⁷⁰ Ine ndikungoyesetsa kuti nditengere Uthenga kwa anthu. Ine ndikuyesetsa kuti ndikupangitseni inu kuwona chenichenicho...Ngati inu muchiritsidwa; mwina, ngati mungakhale moyo nthawi yayitali, mudzadwalanso nthawi ina. Koma ngati mudzapulumutsidwe konse, inu muli nawo Moyo Wamuyaya. Mukuona? Inu mukhoza kuchiritsidwa, ndi kupita pa njira yanu ndi kutaya chipulumutso chanu... inu mukhoza kutaya moyo wanu, kani; koma pamene inu mwapulumutsidwa, inu muli nawo Moyo Wamuyaya pamenepo, kuti simudzadwalanso.

¹⁷¹ Ine ndikudabwa ngati inu munamvetsetsa usikuuno chimene ine ndimachikamba, kuti Mulungu anawonekera kwa Abrahamu ndi Sarah kumeneko, ndipo anawapatsa iwo chizindikiro chotsiriza, Mngelo uja, kuti chiwonongekocho chisanabwere ndipo mwana wolonjezedwayo asanaperekedwe. Kwa Mpingo, icho, chizindikiro chimenecho, chinali Mwana amene anali nkudza. Kwa dziko, chinali chiwonongeko. Tsopano, chimene Iye anamuchitira Abrahamu ndi iwo chinali zitsanzo.

¹⁷² Yesu anabwera pa dziko lapansi, Mbewu yachifumu ya Abrahamu, ndipo anadzachita chizindikiro chomwecho. Ndi angati akudziwa kuti izo ndi choncho, nenani "Ameni." [Osonkhana akuti, "Ameni."—Mkonzi]. Ndithudi. Ndipo iwo anakana icho. Nkulondola uko?

¹⁷³ Tsopano, Iye sanachite konse zimenezo kwa Amitundu, chifukwa Mbewu yachifumu inali isanatulukire, Mpingo unali usanabadwebe. Koma pamene Mpingo unadzabadwa, ndipo tsopano iwo wakhala ndi zaka thuu sauzande, basi pa... Kumbukirani, apo panali kumapeto kwa kuyembekezera kwa Abrahamu. Uko kunali kutseka kwa mbewu yachibadwa ikuyembekezera Mesiya, chifukwa Mesiya anali pamenepo.

¹⁷⁴ Uku ndi kutsekera kwa kudikira kwa Mbewu yachifumu. Iye ali pano, kuwonekera kwa Khristu. Kodi inu munayamba mwayeserapo kugawa...Muli malo mu Baibulo, inu mukudziwa, ndiribe nthawi yoti ndipite mu zimenezo, amati "kuwonekera kwa Khristu," ndipo kenako "Kudza kwa Khristu." Zimenezo ndi zinthu ziwiri zosiyana, pamodzi, "kuwonekera" ndi "Kudza." Iye akuwonekera tsopano,

akugwira ntchito ndi ife mu mawonekedwe a Mzimu Woyera, kuwupanga iwo kukhala wangwiro basi, Mpingo. Iwo ukuyenera kutero.

¹⁷⁵ Monga ngati muli ndi ndalama ya dola mthumba mwanu, itulutsemi iyo ndipo muyang'ane. Mbali imodzi ndi chisindikizo cha Amerika; mbali yinayo ndi chisindikizo cha Igupto, piramidi yokhala ndi mwala wapamutu pamwamba pake, ngati diso likuyang'ana. Ndipo chifukwa chiyani dola ya Amerika anayika panso pamene, “Chisindikizo chachikulu”? Zikuwoneka ngati chisindikizo cha Amerika chingakhale chisindikizo chachikulu kuno. Koma Boma la United States limazindikira izo kaya iwo akuchifuna kapena ayi, chisindikizo chachikululo.

¹⁷⁶ Penyani piramidi imeneyo pamene ikuwumbika, Mpingo. Kulungamitsidwa, kuyeretsedwa, ubatizo wa Mzimu Woyera, ndipo kenako izo zikuyenera kusongoka mpaka pamene... Mwalawapamutu sunafike pa piramidi, Iwo unakanidwa, monga ngati Mwalawapangodya. Tsopano, koma pamene Mwalawapamutu uwo ubwera... Ine ndafikapo ku piramidi; ndi zokwanira mwangwiro basi, inu simungathe kuyendetsa lumo pakati pake, pamene pamakhala matope. Ndipo pamene Mpingo ubwera, ndizo... Pamene Khristu adzabwera kudzawulandira Mpingo Wake, Mpingo udzakhala ndi utumiki ndendende basi monga choncho, ndipo kudzera mu chisomo chimenecho udzawukitsa chinthu chonsecho, kenako nkumapita. Kubwera kwa Mwalawapamutu; kulira, “Chisomo, kwa Ambuye!”

¹⁷⁷ Ine ndiri ndi chinachake mmalingaliro anga. Aleluya! Mulungu wathu akanali Mulungu. Iye amaulula zinsinsi Zake kwa antchito Ake. Ine ndinayankhula za Mngelo amene anatembenezira nsana Wake ku hema, ndipo anali atatembenzira nsana Wake ku hema, ndipo ananena chimene Sarah ankaganiza mkati. Ine ndikuneneratu kuti Mngelo ameneyo ali pano tsopano, Mzimu Woyera, Lawi la Moto lomwelo, Mmodzi yemwe uja amene anali mwa Khristu. Lawi la Moto linawatsogolera ana a Israeli. Lawi la Moto linapangidwa thupi ndipo linadzakhala pakati pathu. Iye anati, “Ine ndinachokera kwa Mulungu, ndikupita kwa Mulungu.”

¹⁷⁸ Itachitika imfa Yake, kuikidwa mmanda, chiukitsiro, kukwera kumwamba, Iye anakumana ndi Saulo pa njira yopita ku Damasiko. Ndipo Kuwala kunamugwetsera iye panso. Ndipo iye anati, “Ambuye, Ambuye!”

¹⁷⁹ Iye anati, “Saulo, Saulo,” choyamba. “Ndani ali... Chifukwa chiyani iwe ukundizunza Ine?”

Anati, “Inuyo ndi Ndani, Ambuye?”

Iye anati, “Ndine Yesu.” Anabwerera!

¹⁸⁰ Apa Iye ali pano usikuuno, wotsimikiziridwa ndi Mpingo Wake, mwasayansi ndi zonse! Oh, abwenzi, nchifukwa chiyani ife tiri opusa chomwecho? Nchifukwa chiyani timakhala

otsika chonchi? Mulole a—mulole Mulungu amene anayankhula Mawu, mulole Mulungu amene. . . Monga Elisha ananena, amene anabwerera ndi magawo awiri a Eliya, anapinda chovala, ndipo anati, “Ali kuti Mulungu wa Eliya?” Mulole Mulungu amene analemba Mawu, awatsimikizire Mawu! Ngati Awa ali Mawu Ake, muloleni Iye ayime ndi Iwo! Iye analonjeza kuti adzachita izo. Iye adzachita izo ngati ife tikhulupirira izo.

¹⁸¹ Tsopano ndiloleni ine ndifotokoze izi momveka bwino. Ine sindine Munthu ameneyo. Ine ndi wantchito wa Munthu ameneyo. Ndipo inunso muli, nanunso, ngati ndinu Mbewu ya Abrahamu.

¹⁸² Koma, ine ndikulalikira Mawu Ake, ndipo ndikuyima mu tsiku limene chipembedzo chirichonse chandikana ine, mabungwe akundithamangitsa kuchoka kumalo kupita kumalo. Ndipo abale ofunika basi amene ali mu mabungwe amenewo, amene amawona Kuwala, adzagwiritsitsa kwa Iko mosalabadira zimene malikulu akunena. Mulungu adalitse amuna monga amenewo. Mulungu adalitse akazi ndi amuna amene anayima usiku watha. Kodi ine ndingakuchitireni inu chiyani? Ndifunsi ine chinachake. Ndifunsi ine choti ndichite, ndichita chirichonse chimene ndingathe kwa inu. Inu ndi anthu a Mulungu. Mwamuna kapena mkazi aliyense angapange mayimidwe monga amenewo, mkati mwa mkangano, ine ndiri ndi ulemu kwa inu.

¹⁸³ Tsopano ngati Mngelo ameneyo. . . Mu Mawu a Yesu Khristu izo zinaneneratu, kuti kudza kwa Mwana wa munthu kusanachitike, kuti chinthu chomwecho chimene chinachitika ku Sodomu chikadzachitika ku Mpingo, muloleni Iye abwere powonekera.

¹⁸⁴ Ine nditembenuza nsana wanga. Inu muweramitse mutu wanu ndipo muzipemphera. Ine sindinganene konse izi ngati sindinamverere kutsogozedwa kuti ndichite izo. Ndingakhale wopusa kunena mawu otero. Koma, kukhulupirira mwa Khristu Mwana wa Mulungu, kukhulupirira kuti Iye ndi Mawu! Ndipo Mawu amapangidwa chenicheni mu thupi lathu, pamene ife titenga Mawu, chifukwa ndi lonjezo Lake, “Ine ndidzakhala mwa inu mpaka kumapeto a dziko, ndipo ntchito zimene Ine ndikuzichita inunso mudzazichita.”

¹⁸⁵ Ine ndatembenezira nsana wanga kwa omvetsera, Atate Akumwamba, amene ine ndawalalikira, pa Uthenga uwu. Ine ndikukupemphani Inu, Mulungu, mulole izo zidziwike usikuuno kuti Inu mukanali Yesu Khristu Mwana wa Mulungu, ndipo Inu mukanali Yehova Mulungu. Ndinu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ndipo munali Inu pamenepo mukuyankhula kwa Abrahamu tsiku lija pa hema. Munali Inu amene munkatha kuzindikira chimene mkazi ameneyo ankaganiza mu hema, ndi kumuuzza iye. Ndipo

pomwepo, iye akukana izo, Inu mukanakhoza kuwuchotsa moyo wake, koma iye anali gawo la Abrahamu, mkwatibwi wake. Ambuye, Inu mukanachotsa miyoyo yathu, chifukwa cha kusakhulupirira kwathu, koma ndife gawo la Khristu. Inu simukanatha kutenga, kumutenga Sarah popanda kumupweteka Abrahamu. Ndipo Inu simungawutenge Mpingo ndi—popanda kumuvulaza Khristu. Ndithandizeni ine, Ambuye. Ine ndiribe maphunziro. Ndine basi. . . Ambuye, ine ndiribe kalikonse, koma ndingokukhulupirirani Inu. Ndipo ine ndikukhulupirira. Ndithandizeni zimenezo, Ambuye.

¹⁸⁶ [Mlongo akuyankhula mmalirime, mlongo wina akutanthauzira—Mkonzi]. Ameni. Mathokozi akhale kwa Mulungu wamoyo. Tsopano, Iye alipo. Mukhale molemekeza, aulemu.

¹⁸⁷ Inu mukhoza kukweza mutu wanu ngati mukufuna. Tsopano osati kokha. . . Mwaona, Baibulo limanena kuti kuyankhula mmalirime ndi kungozimangiriza wekha, pokhapokha patakhalala kutanthauzira. Ndipo ngati kutanthauzira, umenewo ndi uneneri kwa Mpingo. Ndipo momwe ine ndinamvera kutanthauzira kumeneko ndiye, kunali “Khulupirirani Ambuye, kuti ndi Iye amene watumiza Mawu.” Ndipo kenako ine sindinabwere konse mu dzina langa lomwe, ine ndabwera mu Dzina Lake. Ndipo ntchito Zake Iye akanadzazichita kudzera mwa ine pamenepo, polalikira Mawu Ake ndi kutsimikizira Mawu Ake. Ndithudi. Ine ndikukhulupirira zimenezo. Inu mukukhulupirira zomwezo? Ndi angati akukhulupirira zimenezo tsopano, Iye asana. . . ? Mulungu akudalitseni inu. Tsopano, njira yake ndi imeneyo, ndiyo njira yake. Musunge mlingo womwewo ndipo muwona chinachake chikuchitika.

¹⁸⁸ Ine nditembenuzira nsana wanga kwa omvetsera, chifukwa umenewo unali Mzimu Woyera ukungochitira umboni kwa izo. Mukuona? Khalani amphamvu ndi choti muchite. Tsopano inu mukhulupirire kunja uko mwa omvetsera, winawake. Palibe munthu amene ndingamuwone. . . Ndi angati kunja uko amene akudwala ndi osautsika, kapena ali ndi winawake amene akusautsika, kapena chinachake chimzake chimene inu mukuchipempherera, ndipo inu mukudziwa kuti ine sindikudziwa kalikonse za izo, ingokwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino, ndikuganiza kuti ziri paliponso. Chabwino, tiyeni tingokhulupirira tsopano. Musati, aliyense asachokepo, mungondipatsa ine. . . Ndi—ndi maminiti thwelofu kuti ikwane teni. Mundipatse ine maminiti thwelofu, inu mutero? Aliyense asasunthe. Aliyense asachokepo, nkomwe. Mungokhala bata kwenikweni tsopano. Basi nthawi imodzi yokha, tsegulani mtima wanu.

¹⁸⁹ [M'bale akuyankhula mmalirime, m'bale wina akutanthauzira—Mkonzi]. Ameni. Zikomo Inu, Ambuye, zikomo Inu. Mwaulemu tikulemekeza zimenezo ndi mtima

wathu wonse. Imeneyo ndi mphatso mu Mpingo. Mungokhala mu pemphero, molemekeza.

¹⁹⁰ Kumbukirani, iwo ankapita ku nkondo nthawi ina, iwo sankadziwa momwe angakumanirane ndi nkondo yaikulu iyi. Davide anali atayima pamenepo, ndipo anawagawira iwo chidutswa cha nyama ndi dende la vinyo. Koma Mzimu unagwera pa munthu mmodzi, ndipo iye analosera ndipo anawauza iwo poti akakomane ndi mdani, ndipo izo zinali chomwecho.

¹⁹¹ Ife tikukumana ndi nkondo yayikulu, m'bale. Ndipo ife tikuyima mu nkondo yayikulu pakali pano. Mzimu wagwa ndipo, pa winawake, ndipo wakuuzani inu choti muchite, kuti “mukhulupirire.” Iye akuyesetsa kuchotsa malingaliro anu kuti asakhale ine. Mukuona? Ena a inu mukuyenera kumaganiza kuti ndi M'bale Branham akuyesera kuti achite chinachake. Si ine; ndi Iyeyo. Ine basi. . . Mphatso ndi kungodzipereka wekha, monga kudzikokera wekha mu giya. Chimodzimodzi monga maikrofoni iyi, mukaiyatsa iyo, chinachake chikuyenera kuyankhula kudzera mwa iyo. Ndi kagiya kakang'ono kamene ndimayatsa, kanthu kakang'ono. Mzimu Woyera! Ine sindimayatsa; Iyeyo amayatsa. Ndipo kenako Iye amayankhula; si ineyo. Tsopano mukhale molemekeza ndipo mukhulupirire, aliyense wa inu, ndipo muzingopemphera.

¹⁹² Tsopano, aliyense akudziwa kuti Baibulo linanena kuti “Yesu Kristu pakali pano ndi Wansembe Wamkulu amene amakhudzidwa ndi kumverera kwa zofooka zathu.” Ngati izo ziri zoono, mulole osonkhana anene, “Ameni.” [Osonkhana akuti “Ameni!”—Mkonzi]. Kodi Iye ndi Wansembe Wamkulu yemweyo? Nenani, “Ameni.” [“Ameni!”] Ngati Iye ali Wansembe Wamkulu yemweyo, Iye angachite mwanjira yomweyo. Nkulondola uko? [“Ameni!”] Ameni. Tsopano kodi inu mungachite chiyani?

¹⁹³ Tsopano, kundikhudza ine, izo sizingapange kusintha kulikonse; ine ndi munthu. Koma kumukhudza Iye, ndiye Iye ndi Mzimu Woyera umene uli *muno*, ndiye Iye amayankha ndipo amagwiritsa ntchito milomo ya munthu. Chifukwa, Iye ndi Mpesa, ife ndi nthambi; Iye samabala zipatso, Iye amangopereka mphamvu ku nthambi.

¹⁹⁴ Ndizo, ndingotembenuza nsana wanga, kuti muwone kuti zinthu zimene ndazinenazi.

¹⁹⁵ Tsopano, atumiki awa pano pa nsanja, iwo akupemphera. Mukhoza kundiyang'ana ine ngati mukufuna. Izo zonse nzabwino. Kutu mungowona, mukhoza kudziwa kuti iwo ndi basi. . . Chifukwa, ndinu m'busa, ndinu amene mukuweta nkhosa izi. Chotero, kuti inu mudziwe. Ndipo ine ndikufuna kuti inu mundipempherere ine, abale. Chifukwa, inu mukuona chimene ine ndikutanthauza? Ine ndikuyimira Khristu yemweyo

amene inu mukumutumikira. Ndipo ndine m'bale wanu, mzika mzanu wa Ufumu, ndi inu abale. Ndipo ine ndangokhala pano . . .

¹⁹⁶ Mwaona, tsopano, pakali pano Mawu amene ine ndinalalikira, mwaona, Iwo ali pachiwopsyezo. Pakali pano, kulephera, ndicho chimene Satana angafune kuwona. Ndizo zonse zimene iye akufuna. Koma Mulungu si wolephera. Mungokhala olemekeza.

¹⁹⁷ Tsopano nditatembenusa nsana wanga, ndikufuna winawake. . . Ndiloleni ine nditembenuze iwo, ndi njira yonse mozungulira. Mundilole ine nditembenukire ku gawo ili, choyamba, ndipo kenako ndibwera ku gawo linalo. Tsopano winawake kumbuyo mbali iyi; pali ochuluka, monga, akupemphera. Mmbuyo mbali iyi, winawake apemphere kumbuyo kuno tsopano, amene akufuna kuti amukhulupirire Mulungu. Mungokhulupirira ndi mtima wanu wonse, kumbuyo kuno kwinakwake.

¹⁹⁸ Tsopano, Atate Akumwamba, ine—ine ndikukuyamikirani Inu mu mauthenga Anu onse, chirichonse chimene Inu mwachita. Tsopano ndithandizeni ine, Ambuye. Ndine—ndine. . . mwa chikhulupiriro, ine ndikukukhulupirirani Inu, Mawu Anu. Ine ndikukhulupirira Iwo unali Mzimu Wanu umene unandiyitana ine kuti ndichite izi. Tsopano lolani kuti chidziwike kuti ine ndayankhula Choonadi. Ine ndachitira umboni za Inu, tsopano chitirani umboni, Ambuye, kuti ine ndinanena Choonadi. Ine ndikupempha izi mu Dzina la Yesu. Amen.

[Mlango akuyankhula mmalirime—Mkonzi].

¹⁹⁹ Atate Mulungu, ife tikuyembekezera kutanthauzira kwa izo. Inu munanena, mu Baibulo, pamenepo padzikhala “atu,” ndipo ilo ndi lachitatu. Tsopano ife—ife tikupemphera kuti—kuti Inu mudziwitsa izo kwa winawake amene ali ndi mphatso za kutanthauzira. Ine ndikudzisiyira izo kwa Inu, mu Dzina la Khristu.

[M'bale akupereka ulosi—Mkonzi]. Zikomo Inu, Ambuye.

²⁰⁰ Tsopano, uwo unali ulosi, osati kutanthauzira. Mwaona, iye wanena zochuluka kuposa zimene mkaziyo ananena. Pali kutanthauzira kukubwera. Mwaona, munthu ameneyo anali mneneri.

²⁰¹ [M'bale akutanthauzira—Mkonzi]. Amen. Zikomo Inu, Ambuye.

Molunjika kumbuyo kwanga . . .

²⁰² [Mlango akupemphera—Mkonzi]. Mulungu, perekani mdalitso kwa mkaziyo, iye akuwulirira. Mungokhala . . .

²⁰³ Tsopano mungokhala olemekeza kwenikweni tsopano, ndipo mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse. Tsopano, mwa Mzimu

Woyera, ine ndikuyesetsa kuti ndibweretse Mawu amene ine ndalalikira, mmene Iye wachitira umboni kuti chidzachitika. Tsopano mukhulupirire ndi mtima wanu wonse.

²⁰⁴ Pali winawake wayima patsogolo panga, amene wakhala kumbuyo kwanga. Ndipo ndi mkazi. Ndipo iye akuvutika ndi vuto la mtima. Ndipo ali ndi ziwengo zomwe zikumuvutitsa iye. Iye ali kumbuyo kwanga. Ngati mkaziyo sakuimirabe...Omvetsera akuyang'ana; maso anga ndi otseka. Iye akukhudzidwanso ndi wokondedwa, ameneyo ndi, mwamuna wake amene wakhala pambali pake; iye ndi wopuwala, ali ndi ndodo. Dzina la mkaziyo ndi Akazi a Brumley. Mukhulupirire ndi mtima wanu wonse. Imirirani ndipo muvomereze zimene mwapempherera, ndipo mupeza chimene mwapempha. Imirirani pa mapazi anu. Iye waimirira? [Osonkhana akuti, "Inde."—Mkonzi].

²⁰⁵ Mulungu akudalitseni inu. Ine sindikumudziwa mkaziyo, sindinamuwonepo iye mmoyo wanga. Ndife alendo kwa wina ndi mzake. Apo pali...Tsopano afunseni iwo, pitani ndipo mukawafunse iwo ngati ziri zoono. Tsopano ngati uyo sali Mulungu yemweyo amene anali kumusi uko pamaso pa Sodomu, ine sindikudziwa chimene icho chiri.

²⁰⁶ Winawakenso mu gawo ili mukhulupirire tsopano ndi mtima wanu wonse. Ambuye Yesu. Pali mkazi wakhala kumbuyo kwanga. Iye ali ndi chokhumba chakuya. Iye akupempherera chinachake kuti Mulungu amupatse iye. Ndi mwana, yemwe iye akumupempherera. Iye ali pomwe apa kumbuyo kwanga. Akazi a Holm, inu muimirire ndipo mukhulupirire Ambuye Mulungu. Ndipo ngati inu muti mukhulupirire izo ndi mtima wanu wonse, inu mukhoza kukhala naye mwana amene inu mukumupempherayo.

²⁰⁷ Mkazi akubwera, ndipo ndi wolumala. Iye wakhala pa chikuku. Ali kumbuyo kwanga. Iye si wochokera kudera lino la dziko. Iye akuchokera—ndi wochokera ku Sacramento, kumpoto kwa Sacramento. Iye wadwalika kwambiri. Madokotala sakumuthandiza iye. Iye wakhala ali mchipatala. Iye anali maoparesoni angapo. Iye ali ndi vuto la impyso, vuto ndi mafupa ake. Iye akungokhala wamanjenje, mpaka iye ali ndi zovuta. Iye wayipa kwambiri. Akazi a Beeler, pamenepo, kwezani mmwamba dzanja lanu ndipo mukhulupirire kuti Ambuye Yesu...ndipo akupangeni...Mulungu akudalitseni inu.

²⁰⁸ Inu mukukhulupirira? Mulungu akadali moyo ndipo akulamulira. Ngati inu mukukhulupirira izo ndi mtima wanu wonse!

²⁰⁹ Apa pali mkazi wamng'ono, ine ndikuyang'ana pa iye wakhala apa. Iye ali ndi vuto la matumbo. Dzina lake, ine sindikumudziwa iye. Koma kodi iwe ukukhulupirira Mulungu

akhoza kundiuza ine chimene iwe uli, dona? Akazi a Berglund. Iwe ukhulupirire ndi mtima wako wonse, ndipo iwe ukhoza kuchiritsidwa. Iwe ukhulupirire.

²¹⁰ Apa pali dona wakhala pomwe pano, akumupempherera mzake amene wangochita ngozi kumene. Iwe ukukhulupirira ndi mtima wako wonse, iwe ukhoza kukhala nacho chimene iwe wapempha.

²¹¹ Pali dona wakhala pamenepo akudwala mutu. Kodi iwe ukukhulupirira ndi mtima wako wonse? Iwe ukhoza kuchiritsidwa. Usakayikire izo. Ungokhulupirira. Ngati Iye sali Mulungu yemweyo, ine sindikudziwa chimene Iye ali. Iye ali pano ku—ku, ngati iwe ungavomereze izo ndi kukhulupirira izo.

²¹² [Mlongo akuyankhula mmalirime, m'bale akutanthauzira—Mkonzi]. Amen. Ambuye alemekezeke.

²¹³ Kodi inu simukuzindikira kuti muli mu Kukhalapo kwa Mulungu? Inu muchite zimenezo. Tsopano ine ndikuganiza chimene tikuyenera kuchita pakali pano, Mzimu utatha kuyankhula, “Bwerani kwa Ine, ndikhulupirireni Ine, anthu Anga,” Ine ndikuganiza ife tiyenera kuyimirira kuyitanira kuguwa pakali pano, ndipo mulole iwo amene sakumudziwa Khristu abwere adzazungulire guwali pano ndi kumulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu. Ngati inu simunalandire Mzimu Woyera, inu mubwere, nanunso, kuti mudzalandire Mzimu Woyera, chifukwa icho ndi chimene chiti chichitike. Kodi inu simubwera tsopano pamene ife tikupeza poyambira; winawake atsogolera kuyimba. Mzimu Woyera wakhala ukuyankhula. Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Uko nkulondola. Winawake atuluke ndi dona apa. Mubwere kuno mukachipeza chimenecho... Mulungu akudalitseni inu, mlongo. Mu Kukhalapo, kumene Baibulo, Mawu, chitsimikiziro, mphatso, chirichonse chikugwira ntchito, kodi icho sichodabwitsa pakali pano? Bwerani mpaka ku guwa. Tsikani pansu muchoke mmakondewo. Inu amene mulibe Mulungu, mulibe kudzazidwa ndi Mzimu, bwerani tsopano pamene ife tikuyimba.

Yesu akudutsa njira iyi,
Njira iyi, lero;
Yesu akudutsa njira iyi,
Iye akudutsa njira iyi lero.

Yesu akudutsa njira iyi,

Kodi inu simubwera tsopano pamene Iye akudutsa, Mzimu Wake ukuyenda, ukuti, “Bwerani”?

... lero;
Yesu akudutsa njira iyi,
Iye akudutsa njira iyi lero.

²¹⁴ Kodi inu simubwera pamene Iye akudutsa? Yang'anani chimene Iye akuchita pakati panu, akuwonetsera kuti Iye ali yemweyo. Sunthirani kunjira komwe, solo iliyonse imene sikumudziwa Iye, imene sinabadwe mwatsopano. Kodi inu simubwera tsopano kuti mudzamufunefune Iye? Kumbukirani, Mzimu Woyera womwewo umakudziwani inu.

. . . njira lero.

Yesu akudutsa njira iyi,
Njira iyi, lero;
Oh, Yesu akudutsa njira iyi,
Iye akudutsa njira iyi lero.

²¹⁵ Tsopano mulole solo iliyonse ibwere tsopano imene sikumudziwa Mulungu, amene simukutsimikiza za maimidwe anu. Bwerani kuno. Musati—musakhale. . . Musakhale ndi kumvetsetsa kwaluntha kwa izo, m'bale, mlongo. Musachite zimenezo. Inu mukhoza kukhala kuti mwachita mtundu uliwonse wa zogirigisha. Inu mukhoza kukhala kuti munali ndi magari mmanja mwanu, pa nkhope yanu, inu mukhoza kukhala kuti munali ndi manjenje, ndi zina zotero. Palibe chotsutsa izo, tsopano, izo ziri bwino. Inu mwina munayankhulapo mmalirime, inu mwina munavinapo mu Mzimu, ndipo nkukataikabe. Izo nzoona. Iwo ukuyenera kukhala Moyo umene wabadwa mwa inu, umene ukutenga Mawu awa ndi kuwapanga Iwo kukhala moyo watsopano kachiwiri. Mwaona, Khristu ndi Mawu. Ndipo ngati inu mulibe chikhulupiriro panobe kuti musunthire mu Mawu amenewo ndi kuwakhulupirira Iwo, kodi inu simubwera tsopano.

²¹⁶ Monga Mpingo wa Mulungu, pamene Kuwala kwa kumadzulo kukuyamba kuwalira pansu, ndipo a—mtengo ukucha; Mulungu anati Iye akanadzabwezeretsa mtengo umenewo, mtengo womwewo wa chipentekoste, Chikhulupiriro cha mtundu womwewo, chirichonse chomwecho chimene iwo anali nacho, mtengo umenewo udzabwezeretsedwanso; popanda chipembedzo, popanda chirichonse, iwo udzabwera mu mphamvu yophweka ya Mzimu Woyera, kuphunzitsa Baibulo ndendende basi momwe Iwo unkachitira izo. Ife tinalonjezedwa umodzi mmasiku otsiriza, inu mukudziwa, kuti udzabwera ndi kudzabwezeretsa Chikhulupiriro chimenecho. Chotero ine ndikukhulupirira Iye ali pano usikuuno, mmawonekedwe a Mzimu Woyera. Bwerani tsopano, pamene ife tikuyimbanso, kuti ife titsimikize kuti takwanitsa izo.

²¹⁷ Tsopano kumbukirani, ngati mizimu iyi. . . Inu anthu Achipentekoste ndithudi mumakhulupirira mphatso zanu za malirime ndi kutanthauzira! Ngati inu simungakhulupirire zimene Iye wachita *pano*, ndiye mukhulupirire malirime anuwo ndi kutanthauzira, za kukuitanirani inu ku guwa. Mulole aliyense abwere. Ngati inu muona *izo* zikugwira ntchito,

izi zikugwira ntchito, Mulungu akugwira ntchito, bwanji, ndi Mulungu! Ndi mochulukira bwanji, apa pali Mawu apa akutsimikizira Izo, akunena kuti Iwo ndi Choonadi. Bwerani. Nthawi ina yowonjezera tsopano, ndipo inu mubwere tsopano.

Yesu akudutsa njira iyi,
Lero, lero;
Yesu akudutsa njira iyi,
Iye akudutsa njira iyi lero.

²¹⁸ Tsopano iwo amene amakhulupirira mwa Mulungu, atumiki enieni overa ndi—ndi antchito a Khristu, bwerani, mukusuntha, pamene ife tikuyimba kachiwiri tsopano. Senderani chapafupi ndi ku guwa, kuzungulira awa apa. Ndipo tiyeni tidzapemphere nawo, limodzi. Bwerani. Simubwera kuno? Ine sindingawafikire iwo, aliyense, ndi manja anga. Ine ndikufuna kuti inu mubwere. Ena a inu abale otumikira mupite pakati pawo kumusi uko tsopano, kuti inu mukakhoze kuwakhudza iwo ndi kuika manja anu pa iwo. Chabwino. Inu amene mukumudziwa Mulungu, bwerani, mukuyenda kuzungulira kuno, ena a inu akazi ndi akazi awa, inu amuna ndi amuna awa. Sunthirani kumtunda kuno tsopano. Ili ndi—a dongosolo la Mulungu. Sunthirani kumtunda tsopano, anthu inu. Izo, ndi zimenezo, nthawi yake ndi imeneyo. Ena a inu amayi aumulungu ndi ena a inu abale aumulungu, sunthirani kumtunda kuzungulira kuno tsopano kuti mudzayike manja anu pa iwo, potsimikizira, kudzayika manja anu pa iwo kuti iwo alandire Mzimu Woyera. Chabwino. Tsopano, ndi zimenezotu. Ndi zimenezotu.

²¹⁹ Tsopano, mwabwera chifukwa chiyani? Chifukwa chakuti inu mukukhulupirira. Inu mukukhutitsidwa kuti Mulungu ali pakati pathu. Iye ali pano usikuuno. Iye ali pano akugwira ntchito mu zizindikiro zazikulu ndi zodabwitsa.

²²⁰ Musunthire chapafupi kwenikweni, aliyense. Musunthire mkati kuti anthu akhale ndi malo ochulukirapo. Musunthire pafupi. Pali ambiri akubwera mu tinjira, inu mwaona. Mungosunthira pafupi.

²²¹ Ndi angati mwa omvetsera akukhudzidwa ndi anthu awa amene ayima pano tsopano, za chipulumutso cha miyoyo yawo? Kwezani mmwamba dzanja lanu. Chabwino. Tiyeni tonse pamodzi tsopano, tikwezere manja athu kwa Mulungu, ndipo tipemphe pemphero.

²²² Atate athu Akumwamba, ife tikubweretsa kwa Inu usikuuno omvetsera awa, ndi Mzimu Woyera pakati pathu, uli pano tsopano, kupanga Mawu Ake kukhala atsopano kachiwiri. Dzazani mtima uliwonse, Ambuye. Mubwere mu mphamvu ya Mzimu. Perekani izi, Ambuye. Mutulutse mantha aliwonse, mdierekezi aliyense. Musunthire mkati mwa mphamvu ya Mulungu, ndipo mutengere miyoyo iyi. Mu Dzina la Yesu

Khristu, ine ndikuwapereka iwo kwa Inu kwa ulemelero Wanu.



62-0706 Yehova-Yire #2
Municipal Auditorium
Grass Valley, California U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. Box 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. Box 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.

www.branham.org